


File 1982

Mulungu Wamoyo

Ndi

Anthu Ace




THE LIVING GOD AND HIS PEOPLE (CHINYANJA)
PUBLISHED BY THE BAPTIST PUBLISHING HOUSE
P. O. BOX 31995, LUSAKA, ZAMBIA

3. Mulungu amayankhula kwa anthu kupyolera mwa kuwerenga mau ace, ndi kupyolera mwa mapemphero.

Mulungu Wamoyo

Ndi

Anthu Ace



THE LIVING GOD AND HIS PEOPLE
(CHINYANJA)

First Published
July 1, 1982

By The
Baptist Publishing House
P.O. Box 31995
Lusaka, Zambia

Written By: Carol Jean Blakely

Printed By
Baptist Printing Ministry
P. O. Box 31995
Lusaka, Zambia

CITSITSIMUTSO CILEPHERA

Koma citsitsimutso cinalephera. Kodi ndi cifukwa ciani Yosiya sadabweretse ku Yuda mapembedzo a Mulungu? Kodi ndi cifukwa ciani Mulungu sadapululumutse anthu ace? Mulungu saka-dakhoza kukhululukira zomwe agogo a Yosiya Manase adacita. Kuyesa kwa Yosiya pa citsitsimutso kudasantha nthawi imene Mulungu adakalanga Israyeli.

Citsitsimutso cidalephereka cifukwa Yosiya adayesa "kupanga" anthu ace kuti apeze citsitsimutso. Mitima ya anthu siidasinthe. Iwo adatulutsa mafano kuwacotsa mu kacisi, koma iwo sadalore Mulungu kuti alowe ku mitima yao. Anthu adamva Buku la malamulo, koma iwo sadalimvere. Iwo anali wonyada ndi kukongola kwa kacisi wao, koma iwo sanali kupembedzeramo Mulungu.

ZINTHU ZOLINGALIRA

Citsitsimutso ceni ceni cimasintha anthu. Mulungu akhoza kukugwiritsani nchito kuti muyambe citsitsimutso mu mpingo wanu. Dziwere-ngani Buku Lopatulika nthawi ndi nthawi. Pemphani Mulungu kuti adzikutsogolerani. Mupempheni kuti asinthe moyo wanu molingana ndi cifuniro cace. Pemphani Mulungu kuti atumize citsitsimutso ku mtima wanu. Mvetserani iye kuti akuyankheni. Ndipo gawirani mzimu wa citsitsimutso ndi Akristu ena.

ZOMWE PHUNZIROLI LITIPHUNZITSA

1. Ngati patati pakhale citsitsimutso, anthu ayenera kuyesa kupembedza Mulungu.
2. Citsitsimutso sicingathe kukakamizidwa pa aliyense.

Hulida, mneneri wa mkazi, adawauza kuti Mulungu adzacita zomwe adalonjeza. Iye adati Mulungu adakalipa pamene anthu ace anali kupembedza mafano. Koma adalonjeza kuwasunga ngati iwo alapa macimo ao.

Yosiya adafuna kuti Yuda amve malamulo a Mulungu. Werengani ndime iyi kuti mupeze zomwe adacita.

(Werengani 2 Mafumu 23:1-5, 21 mukalasi)

MALAMULO A MULUNGU AWERENGEDWA

Mfumu idaitanitsa anthu a Mulungu kufika ku Yerusalemu. Iye adawerengera anthuwo buku la malamulo. Anthu anamvera. Atangotha kuwerengera anthuwo buku, Yosiya adalonjeza kwa Mulungu. Werenganinso ndime 3. Yosiya adatsogolera anthu kuti ayenera kumvera Mulungu. Iwo adati adzacita ziri zonse zomwe Bukulo lidzawauza kuti acite.

MWAYI WACITSITSIMUTSO

Yosiya adaononga mafano onse ndi maguwa wopembedza Baala, Asitarosi, ndi milungu ina yonyenga. Iye adapangitsa kuti aneneri acikunja aphedwe. Fano locititsa manyazi la Ashiroti lidatulutsidwa mu kacisi. Ponena zooni Yosiya ndiye mfumu yokhayo idacita zambiri kupangitsa anthu kuti apembedze Mulungu.

Yosiya adacita cinthu cimodzi cina pobwe- retsa citsitsimutso kudziko lace. Iye adacititsanso phwando la paska. Yosiya adacita phwandolo mu njira ya tanthauzo kwambiri. Phwando limeneli ndi phwando lofunika koposa la Ayuda ngakhale masiku ano.

MULUNGU WAMOYO NDI ANTHU ACE

PHUNZIRO	TSAMBA
1. MASIKU OYAMBA.....	3
2. MPINGO UYAMBIKA.....	7
3. MABVUTO NDI KAKULIDWE.....	12
4. KUYAMBIKA KWA MPINGO	18
5. KULILIRA UFULU.....	22
6. AITANIDWA KUTSOGOLERA.....	27
7. MULUNGU MTHANDIZI WATHU.....	32
8. MTUNDU UPEMBEDZA MULUNGU.....	37
9. ANTHU OSAKHULUPIRIKA - MULUNGU WOKHULUPIRIKA.....	42
10. ANTHU OYERA.....	48
11. MAYENDEDWE OKOMA.....	54
12. KUITANA KODZIPEREKA KWATHUNTHU.....	58
13. KUYESA PA CITSITSIMUTSO.....	63

PHUNZIRO 1

MASIKU OYAMBA

MAU A MULUNGU OPHUNZIRIRA KUNYUMBA: Mateyu
16:18; Luka 1:1-4;
Macitidwe 1-2

MAU A MULUNGU A PHUNZIRO LALERO: Macitidwe
1:1-2; 2:22-32

MAU APAMTIMA: "Ndiponso Ine ndinena kwa iwe, kuti
iwe ndiwe Petro, ndipo pa thanthwe
ili ndidzakhazika mpingo wanga; ndipo
makomo a dziko la akufa sadzaulaka
uwo."

Mateyu 16:18

Buku Lopatulika ndi mau a Mulungu. Lima-
tiuza momwe mpingo unayambira. Liu
lakuti "mpingo" limatanthauza anthu osonkhana.
Mpingo unapangidwa ndi anthu apadera. Mulungu
anawapulumutsa iwo. Iwo anabatizidwa kuonetsa
dziko kuti amakhulupirira mwa Yesu.

(Werengani Macitidwe 1:1-2 mukalasi)

KUPITIRIZA NCHITO YA YESU

Luka, okhulupirira wa Amitundu, analemba
buku la uthenga wa Luka ndi Macitidwe. Anale-
mbera bwenzi lace Teofilo. Luka anafuna kuti
Teofilo adziwe Yesu nayenso.

Mu ndime 1, Luka anakumbutsa Teofilo za
buku loyamba limene anamulemba. Linali la
za Yesu. Yesu anauza ophunzira ace kuti
akhale mu Yerusalemu kufikira atalandira
"lonjezano locokera kwa Atate" (Macitidwe 1:4).
Yesu ananenanso kuti Mzimu Woyera adzabwera
pa ophunzira, ndikuwapatsa mphamvu yogwirira
nchito yace. (Werengani Macitidwe 1:8 kucoke-
ra mu Buku Lopatulika lanu.)

KUFUNIKA KWACE KWA CITSITSIMUTSO

Mu caka ca 722 B.C. Israyeli ufumu wa ku
mphoto unagonjetsedwa. Sudakhoze kukhalanso
wa mphamvu, Yuda ufumu wa ku m'mwera, siuda-
phunzire kucokera pakugwa kwa Aisrayeli.

Yuda nayenso adacoka nasiya njira za
Mulungu. Agogo a Yosiya, mfumu Manase, adama-
nga mafano mu kacisi. Atate a Yosiya, mfumu
Amoni, adatsatira njira zoipa za Manase.
Kacisi sanali kupembedzeranso Mulungu.

Motero Yosiya adapempha anthu kuti amupa-
tse ndalama zokonzetsera kacisi. Anthu adape-
reka zokwanira zokhoza kulemba a nchito.
Nchito idayambidwa. Yosiya adayembekeza kuti
Yuda akhoza kubwereranso kwa Mulungu pamene
kacisi atakonzedwanso.

Pamene anali kukonza kacisi, Hilikiya
adapeza Buku la malamulo.

(Werengani 2 Mafumu 22:8-11 ku kalasi)

MALAMULO A MULUNGU APEZEKA

Buku la Malamulo lidataika cifukwa Yuda
sanali kuligwiritsa nchito. Anthu masiku ano
akasiya kuwerenga mau a Mulungu, amawataya.
Anthu a Mulungu adasiya kupembedza Mulungu
zaka zambiri zapitazo.

Hilikiya anali wokondwa pamene adapeza
Bukulo. Iye adakonda zomwe adaziwerenga.
Nthawi yomweyo adauza mfumu Yosiya. Yosiya
adauza Safani kuti amwerengere Bukulo. Yosiya
adakhumudwa pamene adamva bukulo. Iye adadziwa
kuti anthu ace sadamvere Mulungu. Kodi iye
akadacita ciani?

Mfumu inadabwa ndi Bukulo. Iye adatumiza
uthenga kwa m'neneri wa mkazi wa ku Yerusalemu.

PHUNZIRO 13

KUYESA PA CITSITSIMUTSO

NDIME ZOPHUNZIRIRA KUNYUMBA: 2 Mafumu 22:1-23;
30

NDIME ZA MPHUNZIRO LELERO: 2 Mafumu 22:8-11;
2 Mafumu 23:1-5,21

MAU APAMTIMA: "Niima mfumu paciunda, nicita pangano
pamaso pa Yehova, kutsata Yehova, ndi
kusunga malamulo ace, ndi mboni zace,
ndi malembo ace, ndi mtima wonse ndi
moyo wonse..."

2 Mafumu 23:3

Wiliyamu ndi Yosefe tsiku lina adakumana
mu msika. Onsewo anali ziwalo za mpingo wa
Baptist wa pa mudzi wa pafupi.

Mpingo wa Wiliyamu unali ndi citsitsimutso.
Anthu ambiri adapulumutsidwa. Mpingo wa Yosefe
unalinso ndi citsitsimutso, koma mpingowo
sudasinthe. "Unali monga msonkhano wina,"
iye adatero. "Panalibe cimene cidaoneka."

Wiliyamu ndi Yosefe anali kulankhula za
zitsitsimutso. Kodi ndi cifukwa ciani mpingo
wina unali ndi citsitsimutso comwe cidasintha
miyoyo ndi mpingo wina sudasinthe? Iwo adako-
nza kuti mphamvu zauzimu za Mulungu zitsogolere
citsitsimutso. Anthu adayenera kukhala olora
kuti adzipereke okha kwathunthu kwa Mulungu.

Phunziro ili likadakhocha kuthandiza
Wiliyamu ndi Yosefe. Ndi la mfumu imene idafu-
na citsitsimutso. Mfumu Yosiya adadzipereka
yekha kuti atsogolere dziko lace kubwerera
kwa Mulungu.

Akuphunzira anakhala ku Yerusalemu lita-
tha phwando la Paska monga momwe Yesu anawau-
zira kucita. Iwo anapemphera kwa masiku
makumi asanu.

Tsiku la makumi asanulo, tsiku la Pente-
kosite, Mzimu Woyera anabwera mwa mphamvu.
Mzimu Woyera anathandiza atumwi kumalankhula
zilankhulo zambiri. Iwo analankhula kwa anthu
ambiri amene anali mu Yerusalemu ku phwando la
Pentekoste.

Ophunzira analibe mtsogoleri weni weni wa
pa Pentekoste. Mzimu Woyera atabwera mwa
mphamvu pa ophunzira, Petro analankhula. Iye
anakhala mutu wa mpingo. Werengani mau awa,
omwe ali gawo la uthenga wa Petro.

(Werengani Macitidwe 2:22-32 mukalasi)

"MUNAPACIKA YESU"

Petro analalikirira kwa anthu a ciYuda.
Panali posakaikitsa kuti ambiri aiwo amene
anamva mau ace anadziwa za Yesu. Iwo anadziwa
za ukuru wace ndi nchito zace zopambana. Yesu
anali kuciza odwala. Iye anali kupanga
akhungu kuti aone. Inali kupangitsa opunduka
minyendo kuti ayende. Iye anali kuturutsa
mizimu yoipa ndi kuukitsa akufa.

Petro anauza anthu amenewa kuti iwo anapha
Yesu. Iwo anamukhomera pa mtanda. Komabe
anacita zonsezi cifukwa Mulungu analola kuti
zicitike.

Yesu sanakhalilire m'manda. Mulungu ana-
muukitsa Kristu kucokera kwa akufa. Mulungu
anamukitsa kuti akhalenso wa moyo. Imfa
siikadakhocha kusunga mwana wa Mulungu.

Petro anauza Ayuda amenewa za kuona Yesu
nthawi zambiri Mulungu atangomuukitsa kwa

Akufa. Komatu Ayuda sakadayenera kungodalira pa zomwe ophunzira anazona. Iwo anali ndi njira ina yopezera coonadi.

MALEMBO ANENA ZA YESU

Petro ananena mau a pa Salmo 16:8-11. Iye anati Davide ndiye adalemba mau a m'Salmo. Mu Salmo, Davide anati m'modzi wa mwa "ana" ace adzakhala Mesiya wa Mulungu. Petro anati Davide sanalembe za iye yekha. Davide analembe za Yesu.

Petro anagwiritsa nchito mau a mu Salmo 16 pa ulaliki wace. Ayuda onse anakonda mfumu Davide. Ngakhale kuti iye anali mfumu, koma anafa. Iye sanaukenso kuti akhale ndi moyo, monga Yesu Kristu anacitira.

Davide anali mneneri - Macitidwe 2:30 amatiuza zimenezi. Mulungu anamuuza coonadi ndi kumupatsa uthenga. Mulungu ananena kuti tsiku lina m'modzi wa ana a Davide adzalamulira m'malo mwace. Ameneyo anali mwana wa Mulungu. Davide anadziwa kuti Mwana wa Mulungu adzaphedwa. Koma Mulungu adzamuukitsa-nso kuti akhale ndi moyo.

Petro anauza Ayuda kuti Davide anali kukamba za Yesu. Zolemba zakale za Ayuda zinanena kuti Mulungu adzaukitsa Yesu kucokera kwa akufa. Petro anadziwa kuti Yesu ali ndi moyo. Iye anamuona ndi kulankhulana naye.

NDIFE MBONI ZA YESU

Petro ndi Akristu ena anacitira umboni za Kristu. Pa tsiku la Pentekoste, Mulungu anawathandiza kuti alankhule zilankhulo zosiyana-siyana. Anauza anthu ocokera ku maiko ambiri za Yesu Kristu. Iwo anakhala ziwalo za mpingo oyamba.

Tikhoza kuswa lamulo tikayesa kupeza ndalama wosazigwirira nchito. Mwina tikhoza kufuna kukhala omveka kapena kudziwika ndi anthu ambiri. Tikhoza kufuna kukhala okondedwa kotero kuti tikakhoza kukhala kamulungu. Maphunziro akhoza kukhala mulungu. Mphamvu ikhoza kukhala mulungu.

Akristu ayenera kusiya kuyesa kupembedza Mulungu ndi kanthu kena. Tiyenera kuika Mulungu kuti akhale woyamba mu miyoyo yathu. Mulungu wathu sangakhale malo aciwiri m'moyo wa wina wace.

ZINTHU ZOLINGALIRA

Bwanji inu? Kodi mumayesa kupembedza Mulungu pa Sande ndi kupembedza milungu ina pakati pa Sabata? Perekani miyoyo yanu kwa Ambuye. Mukhulupirireni kuti akutsogolereni.

ZOMWE PHUNZIROLI LITIPHUNZITSA

1. Anthu a Mulungu samayenera kulora ena kuti awatsogoze njira yocoka kwa Mulungu. Akristu sayenera kupembedza milungu yonama.
2. Milungu yonama idzatilepheretsa ndipo siingapatse zosowa zomwe anthu ali nazo.
3. Mulungu amaitana anthu omwe ali odzipereka kwathunthu kwa iye ndikuonetsa anthu njira yabwino yobwerera kwa Mulungu.
4. Mulungu amalandira aliyense amene amabwere-ra kwa Iye.

Iwo adatsira zitini za madzi khumi ndi ziwiri pamwamba pa guwalo, nyama ndi nkhu, inayandama mu ngalandeyo. Ciri conse cinamizidwa ndi madzi. Zoonadi panalibe cina cikadapsa tsopano!

Ndime 36-37 ipereka pemphero la Eliya. Werengani ndime zimenezi kaciwiri. Poyamba, Eliya adafuna kuti anthu adziwe kuti Mulungu ndiye ndani. Iye anali Mulungu wa Abrahamu, Isaki ndi Israyeli. Kaciwiri, Eliya adapempha Mulungu kulora Israyeli kuti Eliya anali ndani. Eliya adafuna kuti anthu adziwe kuti iye anali kucita zomwe Mulungu adamuza.

MULUNGU AMENE ADAYANKHA

Eliya adapempha Mulungu kuti amumvere kuti anthuwo adziwe zinthu ziwiri. Iwo adayenera kudziwa kuti Mulungu ndi Mulungu. Iwo adayenera kudziwa kuti Mulungu adawakhululukiranso.

Moto wa Ambuye udagwera pa guwapo. "Udayeketsa" kapena kuti kudya nsembe yopserezayo. Udaya nkundi ndi fumbi. Udaumitsa madzi omwe anali mu mcerawo!

SANKHO LIDAPANGIKA

Aisrayeli adacita zomwe Eliya adawauza kuti acite. Iwo adasankha yemwe adayenera kumupembedza. Onse adasankha Mulungu. Iwo adati, "Ambuye, ndiye Mulungu; Ambuye ndiye, Mulungu."

LERO TIYENERA KUSANKHA

Masiku ano timayesedwa ndi milungu yambiri yonama. Tikhoza kumapembedza ndalama, pamene tikhala ndi zocepa kapena tikakhala tiriberetu.

Ngati inu muli Mkristu, inunso, ndinu ciwalo ca mpingo wa Kristu. Tiyenera kuuza ena za Yesu Kristu. Tiyenera kukhala ndi makhalidwe akuti ena adzadziwa kuti Kristu akukhala mwa ife. Tiyenera kukhala mboni zabwino.

Lero pitani ndi kukauza bwenzi lanu kuti Ambuye adakali ndi moyo. Uzani bwenzi ameneyu momwe Yesu Kristu anakupulumutsirani. Pempherani kuti alole Kristu kumupulumutsa. Kapena pempherani kuti nayenso, auze wina wace za Mpulumutsi wathu.

ZINTHU ZOLINGALIRA

Kodi tiri ndi mphamvu yocokera kwa Mulungu yokhalira mboni zace? Kodi ndi cifukwa ciani timacita mantha kucitira umboni? Kodi tinapulumutsidwadi? Kodi Mzimu Woyera anadzaza mwa ife?

ZOMWE PHUNZIROLI LITIPHUNZITSA

1. Pamene Yesu anakhala padziko lapansi pakati pa anthu, anacita zozizwitsa zambiri.
2. Yesu anaphedwa pa mtanda ndikuukanso.
3. Tikakhulupirira mwa Yesu, timakhala ziwalo za mpingo wace. Mpingo uli ngati thupi la Yesu. Umasamalira ziwalo zace, umawaphunzitsa, ndi kuwalimbikitsa.
4. Akristu ali ndi udindo wouza ena momwe Yesu anawapulumutsira, ndi kuthandiza ena kuti akhulupirire mwa Yesu.

PHUNZIRO 2

KUYAMBIKA KWA MPINGO

MAU A MULUNGU OPHUNZIRIRA KUNYUMBA: Macitidwe
6:1-6; Aroma 16:1-6
Aefeso 4:11-16,
1 Timoteo 3:1-13

MAU A MULUNGU APHUNZIRO LALERO: 1 Timoteo
3:1-13

MAU APAMTIMA: "Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi;
ndi ena aneneri; ndi ena alaliki; ndi
ena abusa, ndi ena aphunzitsi; kuti
akonzere oyera mtima ku nchito ya utumi-
ki, kumangirira thupi la Kristu."
Aefeso 4:11-12

Pambuyo pakubwera kwa Mzimu Woyera pa
akuphunzira a Yesu, Petro, analalikira uthenga
odzala ndi mphamvu. Anthu oposa mazana atatu
anapulumsidwa pa tsiku limenelo. Ndiponso,
Mulungu anali kuonjezera anthu mu mpingo tsiku
ndi tsiku amene anali kupulumutsidwa (Macitidwe
2:41,47). Okhulupirira ambiri atsopano analowa
mu mpingo kotero kuti ophunzira anafuna citha-
ndizo. Iwo anafuna cithandizo kuti akhoze
kucita nchito yao ya mapemphero, kulalikira
ndi kuphunzitsa.

Kodi mpingo unacita ciani kuti uwathandi-
ze? (Werengani Macitidwe 6:1-6 kucokera mu Buku
Lopatulika lanu). Mpingo unasankha amuna asanu
ndi awiri kuti agwire nchito yotumikira mpingo.
Kodi mpingo unafuna anthu a mtundu wotani?
Werengani mau awa kuti mupeze yankho.

(Werengani 1 Timoteo 3:1-13 kukalasi)

Aneneri a Baala omwe anali 450 kaculuki-
dwe kawo, ayenera kupha kunzi, ndi kuiika pa
guwa ndipo osasonkha moto pansi pace. Eliya
acitanso cimodzi modzi. Iye aphanso kunzi,
ndikuiika pa guwa la nsembe osasonkha moto
pansi pace. Aneneri onsewo Eliya ndi a Baala
adayenera kupeza moto kuti milungu yao iwatu-
mizire moto wocokera kumwamba. Ndipo amene
angawayankhe ndi moto akhale Mulungu wa
Israyeli. Anthu adati "Mwalankhula bwino."
Onse adabvomereza.

Eliya adalora aneneri a Baala ayese
poyamba. Iwo adapha kunzi yao ndikuiika pa
guwa. Ndipo adayamba kupemphera kwa Baala.
Aneneri onse 450 anali kupemphera kwa Baala.
Iwo adayamba kupemphera m'mamawa kufikira
nthawi yamadzulo. Werengani ndime 27 kuti
muone momwe Eliya anali kuwasekera mulungu
wa Baala!

MULUNGU WA ABRAHAMU, ISAKI, NDI ISRAYELI

Ndipo Eliya adaitana anthu a Mulungu kuti
asendeze pafupi ndi iye. Iye adakonzetsa
guwa loonongekalo kukonzera Mulungu. Iye ada-
tenga miyala khumi ndi iwiri, kuimila mitundu
khumi ndi wiri ya Aisrayeli. Iye adamanga
guwa ndi miyala. Ndipo mneneri adakumba
ngalande yomwe a aizungulitsa guwalo. Iye
adaika moto pansi mwadongosolo la bwino
mozungulitsa miyala ngati kuti iye ayatsa moto.
Kaciwiri Eliya anadula kunziyo nthuli nthuli
ndi kuika nthulizo pa nkunizo. Kodi iye anali
kucita ciani?

Pamenepo Eliya adacita cinthu cacilendo.
Iye adaitana anthu ena kuti adzaze zitindi za
madzi zinai ndi kutsira pa guwalo. Iye adape-
mpa anthuwo kuti atsire madziwo kawiri kena.

Anthu a Mulungu adagawika ku maiko awiri, Yuda ndi Israyeli. Ahabu anali mfumu ya Aisrayeli. Iye adakwatira Jezebeli, mwana wa mkazi wa mfumu ya amitundu. Iye anali kupembedza Baala ndi iye adatsogolera Ahabu kuti apembedze fanolonso.

Mulungu adalanga Israyeli posatumiza mvula. Eliya, m'neneri wa Mulungu, adauza Ahabu za cilangoco. Ahabu anadana ndi Eliya. Iye adaziwadi kuti Mulungu ali ndi Eliya.

Mulungu adatumizanso Eliya kwa Ahabu patapita zaka zitatu ndi theka. Iye adapita ndi uthenga wa Mulungu kwa Ahabu. Werengani ndime zotsatirazi kuti mupeze zomwe Eliya adauza Ahabu.

(Werengani 1 Mafumu 18:1-21,26,36-39 mu kalasi)

KODI MUDZATUMIKIRA YANI?

Pamene Ahabu adaona Eliya, iye adati, "Iwe ndiwe amene ulikubvuta Israyeli" Eliya adauza mfumu kuti iye sanali kubvuta Israyeli, koma kuti mfumu ndiye idatero. Iye adatsogolera anthu kupembedza Baala, ndi kusiya Mulungu.

Eliya anauza Ahabu kuti akumane pa phiri la Karimeli. Ahabu akadayenera kubwera ndi aneneri ace a Baala, ndi onse Israyeli. Eliya adzaonetsa kuti ndani Mulungu wa moyo pamaso pa anthu onse.

Anthu onse adabwera pa phiri la Karimeli. Eliya adalankhula kwa iwo, "Lero muyenera kusankha amene mudzamupembedza, Mulungu kapena Baala." Baala anali mulungu wa acikunjya yemwe Ayuda anali kumupembedza. M'neneri adawafotokozera dongosolo lace.

Paulo analembela Timoteo, "mwana wace mwa cikhulupiriro." Cimeneci citanthauza kuti Paulo anakonda Timoteo monga mwana wace ndipo anayesa kumuphunzitsa iye zinthu zonse zomwe atate angaphunzitse mwana wace, ngakhale kuti Timoteo sanali mwana wace weni weni. Timoteo anatsogozedwa ndi Paulo kuti akhulupirire mwa Yesu. Iye anali "mwana wace mu uzimu." Iye anafuna kuthandiza Timoteo mu nchito yace monga mbusa.

NCHITO YA MBUSA

Mbusa ndi mtsogoleri wa umunthu mu mpingo. Mulungu amalemekeza munthu amene anamuitana kuti akhale mlaliki ndi mbusa. Mbusa alaliki-ra, kuphunzitsa, ndi kuthandiza anthu omwe ali ziwalo za mpingo. Iye ndi "munthu wa Mulungu."

Mbusa ayenera kukhala munthu wa bwino. Pasakhale munthu wina amene anganene kanthu koipa ka za iye. Iye ayenera kukonda anthu kuti akhale m'nyumba mwace kwa nthawi yaifupi. Iye ayenera kuwapempha kuti adye ndi kugona nawo. Nyumba zogona alendo zinali zocepa m'masiku a Paulo ndipo anali malo angozi okhalamo.

Paulo anauza Timoteo kuti mbusa ayenera kukhala mphunzitsi wa Buku Lopatulika wabwino. M'masiku a Paulo, monganso masiku ano, mbusa ayenera kukhala mlaliki wabwino ndi mphunzitsi wabwino. Mbusa akhoza kuphunzitsa bwino kwambiri pokhala ndi moyo wa makhalidwe a Cikristu cabwino, comwe cili citsanzo cabwino pamaso pa ena.

Mbusa ayenera kukhala ndi mkazi m'modzi. Ayenera kukhala okhulupirika kwa mkazi wace. M'masiku amenewo, monganso masiku ano anthu

amene sanali Akristu anali kukhala ndi akazi oposa m'modzi.

Mbusa ayenera kulamulira nyumba yace bwino. Ana ace ayenera kukhala acangu pomumvera. Ngati sangathe kupanga banja lace kuti limumvere, kodi angathandize mpingo bwanji? Ngati munthu sangaphunzitse ana ace kuti adzimumvera, sangatsogolere mpingo wace kuti umvere Kristu.

Mbusa ayenera kugwira nchito kwambiri. Sayenera kulekera nchito ena. Ayenera kukhala woganiza, wamalamulo abwino, okhulupirika ndi okonzeka kuthandiza amene ali osowa. Iye sayenera kukhala woledzera kapena wamukangano. Ayenera kuyesa kukhala wosakhumudwitsa ena, ndi mau oonetsa cifundo. Mbusa ayenera nthawi zonse kukhala wacifundo ndiponso wokonda. Iye sayenera kukonda ndalama koposa momwe akondera Yesu. Komabe mpingo uyenera kumulipira ndalama za mtengo wa nchito yace. Akatero akhoza kupereka nthawi yace yonse kugwira nchito ya mpingo.

Mkristu watsopano sayenera kusankhidwa kukhala mbusa. Iye afunika nthawi yaikuru kuti akule kukhala monga Kristu. Iye afunika nthawi yophunzira. Iye ayenera kudziwa zambiri kuposa anthu ena omwe ali ziwalo za mpingo. Iye ayenera kuphunzitsidwa mau a Mulungu.

Anthu ena omwe siali Akristu ayenera kulankhula zabwino za mbusa. Ngati atatero ndi kucita, akhoza kukhala mbusa wabwino.

NCHITO YA MKULU WA MPINGO

Mkulu wa mpingo akhoza kuchedwa mthandizi wa mbusa. Iye ayenera kukhala munthu wofanana

4. Mulungu adatumiza atsogoleri auzimu kuti adzatsogolere anthu kubwerera kwa iye.

PHUNZIRO 12

KUITANA KODZIPEREKA KWATHUNTHU

NDIME YOPHUNZIRIRA KUNYUMBA: 1 Mafumu 18

NDIME ZA MPHUNZIRO LALERO: 1 Mafumu 18:17-21,
26
1 Mafumu 18:36-39

MAU APAMTIMA: "Mukayika-kayika kufikira liti? Ngati Yehova ndiye Mulungu, mtsateni Iye."
1 Mafumu 18:21

M'moyo wanga onse ndakhala ndikumapita ku mpingo. Atate anga anali akuru a mpingo. Amai anga anali kumaphunzitsa Sande Sukulu ya ana. Ngati ndikafunsidwa kuti "kodi iwe ndiwe Mkristu? ndinali kuyankha kuti "ndithudi ine ndine. Makolo anga ndi Akristu. Motero ine ndine Mkristu." Tsiku lina pamene ndinali ndi zaka 18, ndidapeza cinthu codabwitsa. Ndida-peza kuti ine sindinali Mkristu. Ine ndinali ndisanabvomereze Yesu Kristu kukhala Mpulumutsi wanga. Tsiku limene ndinabvomereza Yesu monga Mpulumutsi wanga, ndidadzipereka ndekha kwa Yesu. Iye adafuna kuti ine ndidzipereke ndekha kwathunthu kwa Iye.

Masiku ano Akristu ambiri sadzipereka okha kwa Mulungu. Iwo amafanana ndi Aisrayeli. Iwo amapatsa Mulungu mbali yocepa koposa onse athunthu. Mulungu amafuna kukhala oyamba mu miyoyo yathu. Iye adafuna kukhala oyamba mu miyoyo ya Aisrayeli.

MFUMU IMENE IDAYENDA

Ngakhale mafumu ao anali kuyenda. Ndime yathu mu 1 Mafumu 11:1-4 tiwerenga za mfumu ina yomwe idalora milungu ina kumusoceretsa.

Solomoni anali ndi akazi ambiri ocokera ku mitundu ina. Iye adakwatirapo wina kucokera ku Aigupto. Akazi ace anali kupembedza mafano. Iwo anali kubweretsa milungu yao pobwera ku Yerusalemu.

Mulungu adacenjeza Solomoni pomakwatira akazi amenewa. Mulungu adadziwa kuti Solomoni akhoza kusiya Mulungu. Solomoni adayamba kupembedza milungu ya akazi ace. Iye adamangiranso kacisi ya milungu yao. Mtima wace udatembenukira kwa milungu ina m'malo mwa Ambuye Mulungu. Ngakhale mfumu idapanduka ndi kupita kusiya Mulungu.

ZINTHU ZOGANIZIRA

Ganizirani za inu eni. Kodi mumapandukira Mulungu mwakumusiya? Pangani khalidwe lomawerenga Buku Lopatulika ndi kumapemphera tsiku ndi tsiku. Pempherani kawiri kawiri ndi Akristu ena. Mudzakhala pafupi ndi Mulungu ngati mumupembedza iye kawiri kawiri.

ZOMWE PHUNZIROLI LITIUZA

1. Masiku ano, Akristu amayesedwa kawiri kawiri kuti ayende njira yosiya Mulungu.
2. Milungu, mafano amene anthu amawatumikira ndi kuwamvera ndi apafupi ndipo atsogolera m'makhalidwe ao atsiku ndi tsiku.
3. Mulungu amatimverabe tikapempha cithandizo tikalapa ndi kutembenukira kwa Iye.

ndi mbusa. Nchito zonsezi zimafunika anthu abwino. (Yerekezani ndime 3 ndi 8).

Akulu a mpingo afunika kukhala ndi cikhulupiriro cozama ca Cikristu. Iwo ayenera kuonetisa ndi njira imene amakhalira kuti ali Akristu.

Akulu a mpingo ayenera kukhala okhulupirika. Iwo sayenera kunena kanthu kena kwa munthu wina, ndi kuuza winanso kanthu kena (kukhala wa m'thira kuwiri). Iwo sayenera kukhala akumwa mowa kapena zoledzeletsa, kapena kukonda ndalama koposa momwe akondera Yesu.

Akulu a mpingo akhale "okhala naco cinsi-nsi ca cikhulupiriro ndicikumbu mtima coona" (ndime 9). Iwo ayenera kusunga coonadi ca Mau a Mulungu. Akatero adzakhala okhulupirika ku mau. Cikumbu mtima cao cidzakhala cabwino. Sadzakhala amanyazi ndi cimene amakhulupirira.

Munthu ayenera kukhala ndi nchito ina ya mu mpingo asanasankhidwe kukhala mkuru wa mpingo. Ngati iye atacita nchitoyo bwino, akhoza kupangidwa kukhala mkuru wa mpingo. Iye ayenera kutsimikiza kukhulupirika kwace kwa Yesu.

AKAZI AZIBUSA NDI AKULU AMPINGO

Mkulu wa mpingo, ayenera kukhala ndi mkazi m'modzi. Ayenera kukhala mai wabwino, ndi okhulupirika pa zonse zomwe acita. Iye ayenera kukamba zoon nthawi zonse. Iye ayenera kukhala wacifundo ndi wothandiza ena.

Banja la mkulu wa mpingo liyenera kumumvera iye. Zikatero adzakhoza kulemekezedwa ndi ena.

Zinthu zimene zimapanga a nchito abwino amumpingo si za mbusa yekha, akuru a mpingo

ndi akazi ao. Ndi zakwa Akristu onse. Ndi zakwa inu ndi inenso.

ZINTHU ZOLINGALIRA

Mulungu anakupatsani matelente ena ndi luntha. Iye amafuna kuti muzigwiritsa luntha limeneli kuti mumulemekeze iye. Kodi mumalora kuti Mulungu agwire nchito kupyolera mwa inu, kucita nchito zina kupyolera mu mpingo? Ngati simutero, pempherani kuti Mulungu akhoza kukugwiritsani nchito. Mukatero perekani utumiki wanu ku mpingo wanu.

ZOMWE PHUNZIROLI LITIPHUNZITSA

1. Mulungu amapatsa munthu aliyense luntha ndi matelenti osiyana. Monga Akristu, tiyenera kuwagwiritsa nchito kulemekeza Mulungu.
2. Ndi Mulungu yekha amene angaitane anthu kuti akhale abusa a mpingo.
3. Mbusa ndi mtsogoleri wa mpingo. Iye ayanera kukhala monga Kristu kudera liri lonse la moyo wace. Iye ayanera kukhala citsanzo ca ena.
4. Mulungu amaitananso anthu kuti akhale akulu ampingo, aphunzitsi ndi kucita nchito ina mu mpingo.
5. Mulungu amaitananso azimai kuti acite nchito zosiyana siyana mu mpingo. Mpingo umafunika azimai a Cikristu ca bwino. Omwe adakwatiwa ndi abusa, akuru ampingo, ndi ena anchito za pa mpingo ayenera kukhala abwino, Akristu okhulupirika.

Aisrayeli adayamba kupembedza Bala ndi Ashitarobi, milungu ya Akanani. Akanani anali kupereka mphatso za mbeu ndi kumacita zacigololo pokondweretsa Mulungu. Ashitarosi, Mulungu wa mkazi wa Akanani anali kulonjeza Akananiwo zokolora zambiri. Iwo adaiwala Mulungu amene adawalonjeza kuwasamalira.

Aisrayeli anali kudziwa malimidwe pang'ono. Iwo anali kupembedza mulungu wa Akanani cifukwa anali kufuna kukhala alimi abwino. Iwo anafuna kukondweretsa Akanani.

Kupembedza kwa Bala kwa Aisrayeli kudukwiitsa Ambuye. Mulungu adawacenjeza za kupembedza milungu ina. Motero Mulungu adalanga Aisrayeli. Iye adalora mitundu ya cidani kudzaononga mbeu zao. Mtundu wa mphamvu wa Aisrayeli udaopa adani ao.

Pamene adani Aisrayeli adapambana powagonjetsa, adalilira thandizo. Mulungu anali ndi cisoni ndi iwo. Iye adatumiza oweruza kudzapulumutsa kucokera kwa adani ao. Oweruza anali anthu oitanidwa ndi Mulungu kuti adzapulumutse anthu obvutika. Aisrayeli anali kuyang'ana kwa oweruza monga atsogoleri auzimu.

Anthu a Mulungu sadaphunzire pamene Mulungu adawalanga. Iwo adapitirizabe kucimwira Mulungu. Ndipo Mulungu adawalanga polora kuti adani awayambe. Kaciwirinso Aisrayeli adapempha thandizo kucoka kwa Mulungu pamene iwo adagonjetsedwa. Mulungu adatumiza Oweruza kudzapulumutsa, ndi ciyembekezo cakuti abwerera kwa Iye. Komabe Aisrayeli adayenda mosiyana ndi Mulungu.

(Werengani 1 Mafumu 11:1-4 ku kalasi)

anthu ace. Mulungu adawakumbutsa Aisrayeli kuti adawauza kusacita pangano ndi Akanani. Aisrayeli sadamvere Mulungu. Moteru Mulungu adawauza kuti iye sadzaturutsa Akanani. Iwo adzakhala adani Aisrayeli kuti adziyambitsa mabvuto pakati pao.

Yoswa adaika citsanzo cabwino kwa anthu a Mulungu. "Ndipo anthuwo anatumikira Yehova masiku onse a Yoswa, ndi masiku onse a akulu akulu otsala atafa Yoswa, amene adaona nchito yaikuru yonse ya Yehova anaicitira Aisrayeli" (Oweruza 2:7).

Yoswa atangofa, ndi akulu atangofa, fuko latsopano lidakula omwe sanali kutsata mapanga-no omwe adacitika ndi Mulungu. Iwo adatembenuka kucoka kwa Mulungu ndi kuyamba kupembadza mafano. (Werengani Oweruza 2:10-16 kukalasi)

CIMO LA AISRAYELI

Aisrayeli adacimwira Mulungu. Yoswa atangofa, adayamba kuyenda kusiya Mulungu. Atso-goleri atsopano sanali kupembedza Mulungu. Aisrayeli sanali kuuza ana ao za mphamvu ya nchito ya Mulungu.

Aisrayeli adacipeza capafupi kupembedza milungu ya Akanani. Iwo adafutatira cipembedzo ca atate ao. Iwo adaiwala kuitana komwe Yoswa adacita kuti atumikire Mulungu. Iwo adaiwala lonjezano lakukhala okhulupirika kwa Mulungu.

Aisrayeli adayenda kusiya Mulungu coyamba, pakusiya kupembeza Iye. Mulungu ayembekezera anthu ace kupembedza ndi kumuyamika iye. Ahebri 10:25 ikuti; "Osaleka kusunkhana kwathu pamodzi monga amacita ena. Komatu tidandaulirane, ndi-ko koposa monga momwe muona tsiku liri kuyandikika.

Aisrayeli adaiwala Mulungu. Adafulatira misana yao pa Iye. Iwo adaleka kuphunzitsa ana ao za Mulungu. Iwo adaleka kumukhulupirira Iye.

PHUNZIRO 3

MABVUTO NDI KAKULIDWE

MAU A MULUNGU OPHUNZIRIRA KUNYUMBA: Macitidwe 11:11-18; 15:1-35; 19:23-27; Agalatiya 2:11-16

MAU A MULUNGU APHUNZIRO LALERO: Macitidwe 10:9-16; 11:11-18

MAU APAMTIMA: "Potero Mulungu anapatsa kwa amitundu-nso kutembenukira mtima kumoyo." Macitidwe 11:18b

Akristu a ku Yerusalemu anali kulondedwa kwambiri. Iwo anataya nchito zao. Nthawi zambiri mabanja ao sanali kulankhula nao. Anansi ao mwina sanali kuwayang'ana. Nthawi zambiri anali kumenyedwa ndipo anali kubisala kuti akhale ndi moyo. Akristu onse anacoka ku Yerusalemu kupatulako atumwi okha cifukwa ca kulondedwa londedwa.

Petro anayamba kuyendera mipingo imene inayamba kutatha kulondedwa. Iye anapita ku Luda (Macitidwe 9:32-35); ndipo anapita ku Yopa. Petro anaukitsa Dorika kucokera kwa akufa (Macitidwe 9:36-43), ndi kukhala ndi Simoni wofufuta zikopa. Mulungu anali ndi kanthu kena komwe anafuna Petro aphunzire ku Yopa.

Kazembe wa Boma la Aroma anali kukhala ku Kasaireya, kumpoto kwa Yopa. Korineriyo, mkuru wa asilikali wa ci Roma ku Kaisareya, anali wokhulupirira za Ciyuda. Tsiku lina anaona masomphenya ocokera kwa Mulungu. Mu masomphenya a Korineriyo m'ngelo anamuza kuti atume uthenga kukaitana Simoni Petro kucokera ku Yopa. Anthu ace anayenera kukafunsa Simoni Petro kuti abwere

naye ku Kaisareya. Korineyo anatumiza anthuwo nthawi yomweyo.

Tsiku lina ku Yopa, Petro anakwera pa chindwi pa nyumba kuti akapemphere. Inali ora lacisanu ndi cimodzi. Iye anamva njala koma nthawi yakudya inali isanakwane. Petro anaona masomphenya.

(Werengani Macitidwe 10:9-16 mukalasi)

MASOMPHENYA A PETRO

Iye anaona cinsaru cikutsika kucokera kumwamba comangidwa m'ngodya zonse. Nyama za mitundu yonse, njoka, ndi mbalame zinali pa nsaruyo. Liu linanena kuti Petro, "Uka, ipha nudye." Petro anati sanali kudya ciri conse comwe lamulo la Mose linali kukaniza! Liu linakambanso: "Usachule cakudya ciri conse kuti ndi codetsedwa ngati Mulungu anena kuti ndi coyeretsedwa."

Masomphenya anaonekera kwa Petro katatu. Ndipo cinabwerera kumwamba komwe. Pamene Petro anali kuganizira za masomphenya, anthu a Korineriyo anafika.

Macitidwe 10:19-48 amatiuza kuti Petro anapita ndi anthu a Korineriyo ku Kaisareya. Iye anatenga Akristu asanu ndi m'modzi kuti akakhale mboni.

Pamene Petro anacoka ku Kaisareya, anabwerera ku Yerusalemu. Mpingo unadziwa kuti iye anakalalikira kwa Amitundu ku Kaisareya (Macitidwe 11:1-10).

Akristu a ci Yuda anati kwa Petro, "Munakhala mlendo m'nyumba ya munthu wamitundu osadulidwa, ndiponso munadya naye!"

PHUNZIRO 11

MAYENDEDWE OKOMA

NDIME ZOPHUNZIRIRA KUNYUMBA: Oweruza 2;
1 Mafumu 11

NDIME ZA MPHUNZIRO LALERO: Oweruza 2:7, 10-16
1 Mafumu 11:1-4

MAU APAMTIMA: "Potero, penyani bwino umo muyendera, si monga opanda nzeru, koma monga anzeru; akucita macawi, popeza masiku ali oipa, cifukwa cace musakhale opusa, koma dziwitsani cifuniro ca Ambuye nciani."

Aefeso 5:15-17

Mbusa adaona anthu ena atsopano ali kusunthila ndi kukakhala khomo lapafupi ndi iye. Iye adapita kukawacezera. Iwo adati adacoka kumudzi kwao kudzafuna nchito. Iwo sanali kupita ku mapemphero mu mzinda waukuruwo. Iwo anali otanganidwa kugwira nchito. Iwo anakhala mu mzindamo zaka makumi awiri. Iwo sanapite ndi ana ao kumpingo.

Tsiku lina, mwamuna ndi mkazi adazindikira kuti anali kungoyenda monga anthu otaika mu nkhalango. Iwo adasiya Mulungu kumutulutsa mu miyoyo yao ndipo adalephera kuphunzitsa ana ao za Mulungu. Iwo adabwerera ku mpingo ndi kuka-pembedza Mulungu.

KODI NDI CIFUKWA CIANI AISRAYELI ANALI KUYENDA YENDA

Mulungu adagwiritsa Mose ncito kuti atsogolere Aisrayeli poturuka kwa Aigupto, ndi Yoswa kutsogolera Aisrayeli kuti alowe mu Kenani. Mu Oweruza 2:1-6, Mulungu adalankhula kwa

nthawi zonse amadziwa.

Kodi muli kudziwa wina wace amene sanasiye moyo wace wakale wa ucimo - makhalidwe acikunja, kukhala opanda Mulungu ndi malamulo ace? Monga Akristu, timayenera kukhala zitsanzo zabwino kuti ena adzitsata. Kodi inu ndinu otere?

ZOMWE PHUNZIROLI LITIUZA

1. Pali "mafano" ambiri omwe amayesa Akristu masiku ano kuti awapembedze.
2. Mulungu amafuna anthu ace masiku ano kukhala miyoyo yoyera.
3. Akristu ena a mphamvu amathandiza Akristu ena kukhala miyoyo yoyera pokhala zitsanzo zabwino eni ace.
4. Munthu aliyense ayenera kudzisankhira amene adzamutumikira - Mulungu kapena Satana.

Petro anauza mpingo zomwe zinaoneka. Tsopano werengani ndime iyi ya mau. Kodi Akristu a ciYuda anakhulupirira Petro?

(Werengani Macitidwe 11:11-18 mukalasi)

MZIMU ANANDITUMA

Petro anauza mpingo wa ku Yerusalemu zomwe zinamuonekera. Anthu atatu anabwera kudzamutenga ndi kupita naye ku Kaisareya. Mzimu Woyera anamuuza kupita ndi anthu. Petro sanadandaule cifukwa cakuti anali Amitundu. Akristu a ciYuda asanu ndi m'modzi anapita naye. Pamene anafika ku Kaisareya, anapita kunyumba ya Korineriyo. Iye anawauza kuti m'ngelo anamuuza kuti aitane Simoni Petro. Petro anayamba kuuza Korineriyo ndi banja lace za Yesu Kristu.

Pamene Petro anali kulalikira, Mzimu anagwera pa onse anali m'nyumbamo. Mulungu anapatsa Amitundu mphatso yofanana ndi imene anapatsa atumwi. Petro anauza mpingo wa ku Yerusalemu kuti sanayese kuletsa Mulungu. Pamene mpingo anamva kulankhula kwa Petro, analemekeza Mulungu pa zonse anacita.

(Werengani Macitidwe 11:16-18; 15:5-11; 15:19-21 ku kalasi).

MSONKHANO WA KU YERUSALEMU

Nthawi inapita. Paulo anali atapulumutsi-dwa. Iye anali atayamba nchito yautumiki yaikuru. Poyamba iye anali kulalikira kwa Ayuda okha. Pamene Ayuda sanali kukhulupirira mwa Yesu Kristu, Paulo anakhala otumidwa kwa Amitundu.

Akristu ena a ciYuda anayamba kukhala ndi mabvuto oipa. Iwo anali kulondola mosamalitsa malamulo a Mose asanakhale okhulupirira. Atangotha kukhala Akristu, anayesa kupanga Cikristu kukhala ngati cipembedzo ca ciYuda, cipembedzo cao ca kale. Iwo anayesetsa kupanga Amitundu kuti akhale Ayuda asanakhale Akristu. Ayuda amenewa anali kucedwa "Opanga Ayuda" "cifukwa ca cimeneci. Iwo anali olakwa pocita zimenezi. Iwo anayesetsa kupanga Cikristu kukhala ca malamulo ndi copanda dongosolo, monga momwe ciYuda cinaliri. Yesu anadziwa kuti zimenezi zidakaoneka ndipo anapereka miyambi iwiri mu Mateyu 9:16-17, kucenjeza kuti anthu asayese kukakamiza ziphunzitso zace mu cipembedzo ca ciYuda. Yesu anati ciphunzitso cace ca tsopano cidzaononga cipembedzo ca cakale, cifukwa otsalira a cipembedzo ca ciYuda anakhala oina mitima ndipo sanafune kusintha zomwe anali kucita kale. Ena akadasintha, koma ena sakadakhocha kusintha. Yesu anatanthauza kuti mpingo wace udayenera kukhala waufulu kuti ukule, ndi kufikira ena onse amene akadakhulupirira.

Bungwe la ku Yerusalemu linakomana ku Yerusalemu. Iwo anafunsa Petro ndi Paulo kuti abwere kuti adzawauze pamaso pao. Motero Petro ndi Paulo analankhula. Atatha kumva umboni wao, mpingo unauza Paulo kupitiliza kulalikira Kristu kwa Amitundu.

Paulo anapitiriza kupita maulendo autumiki. Iye anapita dela la Galatiya nthawi zitatu. Pambuyo pace anamva kuti Opanga a ciYuda anali kumipingo ya ku Agalatiya. Paulo analemba kalata kwa mipingo yonse ya ku Galatiya. Werengani ndime iyi, gawo la kalata ya Paulo ku mipingo ya ku Galatiya.

yomwe makolo ao anali kuipembedza. Milungu ya Amori idawayesa.

Yoswa adati anthu sanamvere Mulungu. Iye adati ayenera kusankha yemwe adzamutumikira.

KUSANKHA KWA YOSWA

Anthu adayenera kusankha. Iwo akadasankha kutumikira Mulungu amene adawapulumsa, kapena akadasankha milungu yao ya kale. Yoswa adapempha anthu kuti atsate Mulungu woyera. Iye adapereka citsanzo ca bwino ca kwa anthu. Yoswa adati, "Koma ine ndi apa banja anga, tidzatumikira Ambuye."

MTSOGOLERI WABWINO NDICITSANZO CA BWINO

Mtsogoleri wabwino akhoza kutsogolera anthu kuti amvere malamulo a Mulungu. Mbusa ayenera kupereka citsanzo cabwino ca makhalidwe oyera pamaso pa anthu ace. Mtsogoleri ayenera kuthandiza anthu kuti adzikhala monga Kristu. Paulo adafunsa Akristu a ku Roma kuti adzipereke okha monga "nsembe ya moyo yopatulika ya Mulungu, yoperekedwa ku utumiki wace ndi yokondweretsa Iye."

Anthu adayankha Yoswa. Iwo anali kukumbukira ubwino wa Mulungu. Iwo adati, "Tisankha Ambuye."

Ahebri adalonjeza Mulungu kuti iwo sadzakhala monga mitundu ina yacikunja yoyandikana nayo. Iwo adalonjeza kupembedza ndi kumvera Mulungu yekha.

ZINTHU ZOLINGALIRA

Kodi mumadziwa wina wace amene alikuyesa kubisa macimo ace? Palibe aliyense angathe. Wina wace nthawi zonse amadziwa. Mulungu

"Ciyero" cimatanthauza kuposa kungogani-
zira za Mulungu. Anthu oyera amaganizira za
ena. Malamulo a Mulungu amati anthu a Mulungu
ayenera kucitirana wina ndi m'nzace m'onga
momwe Mulungu amawasungira. Ganizirani bwino
ku mau awa: "Musamaba, kapena kunyenga,
kapena kunamizana. Musamalumbira monama ndi
kuchula dzina langa, ungaipse dzina la Mulungu
wako; Ine ndine Yehova. Usamasautsa m'nansi
wako kapena kulanda zace; mphotho yace ya woli-
pidwa isakhale ndi iwe kufikira m'mawa"
(Levitiko 19:11-13).

Ahebri anali kukhala pakati pa anthu amene
sanali kudziwa Mulungu kapena malamulo ace.
Iwo akadakhala ali kucitira umboni pokhala ndi
miyoyo yangwiro pakati pa anansi ao.

Kodi Akristu ayenera kuyesa kukhala ndi
miyoyo yoyera? Mulungu adatipatsa mau ace
oyenera kuwamvera. Timawerenga mu 1 Petro
1:15-16 kuti, "monga Iye wakuitana inu ali
woyera mtima, khalani inunso oyera mtima m'ma-
khalidwe anu onse; popeza kwalembedwa 'Muzikha-
la oyera mtima, pakuti Ine ndine woyera mtima.'"

KODI MUDZATUMIKIRA YANI?

Aisrayeli sanali kukhala oyera. Iwo
adaiwala Mulungu. Iwo adapanga mafano a milu-
ngu ya Akanani.

Yoswa adakhala mtsogoleri wa Aisrayeli
pamene Mose adafa. Iye adatsogolera Aisrayeli
ku dziko la malonjezano. Anthu a Cikanani
ambiri anali kukhalabe kumeneko. Aisrayeli
anali kukhala pakati pao.

Pamenepo Aisrayeli adaiwa Mulungu. Ena
adabweretsa milungu yao ya ku Aigupto ndi
kuipembedza. Ena anali kupembedza milungu yao

(Werengani Agalatiya 2:11-16 mukalasi)

KHALANI OONA KUCIKHULUPIRIRO CANU

Paulo anamva kuti opanga a ciYuda afika
ku Agalatiya. Iye anafuna kuti Akristu a ku
Agalatiya adziwe momwe iye anacitiridwa ndi
opanga Ciyuda.

Paulo ndi Barnaba anabwerera ku Antiokeya.
Iye anapeza Akristu a ciYuda ndi Amitundu
akudiyera pamodzi. Ayuda sanali kudya kawiri
kawiri ndi Amitundu. Koma Petro anadya ndi
Amitundu ku Antiokeya.

Akristu ena anabwera kucokera ku Yerusa-
lemu. Yakobo anawatumiza. Pamene iwo anafika,
Petro analeka kudya ndi Akristu amitundu.

Paulo analankhula kwa Petro. Iye anati
"ngati inu monga m'Yuda mukhala monga wa
Mitundu, cifukwa ciani kupanga Amitundu kuti
akhale monga Ayuda?" Paulo anathandiza Petro
kukumbukira momwe munthu ali opulumutsidwa.
Munthu sangathe kupulumutsidwa cifukwa comvera
malamulo. Zoonadi, ndi zakuti munthu akhoza
kukhala opulumutsidwa pamene aika cikhulupiriro
cace mwa Mwana wa Mulungu, Yesu Kristu.

ZINTHU ZOYENERA KUGANIZA

Kodi timayesa kupanikiza ci Kristu cathu
munjira zathu za cikunja? Kodi tiri kuyesa
kukhala "olengedwa atsopano mwa Kristu?" Kodi
timayesa kukakamiza ena kuti acite zinthu
zomwe siziphunzitsidwa mu Buku Lopatulika?
Kodi timapanga "malamulo" a mpingo wathu kuti
awatsate kuteroko ndikucotsa ufulu umene Yesu
anatipatsa?

ZOMWE PHUNZIRO LITIPHUNZITSA

1. Cikristu ndi ca anthu onse.
2. Anthu amafuna "kucita" kanthu kena kuti adzipulumutse okha. Ena amapanga malamulo. Ena amayesa kucita zabwino. Koma zinthu zimenezi sizidzapulumutsa aliyense.
3. Munthu akhoza kupulumutsidwa pamene akhulupirira mwa Yesu ndi kukhulupirira Iye kuti amupulumutse.
4. Akristu ayenera kukhala woona mu cikhulupiriro cao mwa Yesu. Umboni wao uyenera kukhala woona pa nthawi zonse.

"Ciyero" cidatanthauza kukhazikidwa pa mbari kapena kupatulidwa kucokera ku kanthu kena kapena cifukwa ca colinga ca padera. "Ciyero ca Mulungu" cinatanthauza kuti iye adanyamulidwa kukhala pamwamba pa anthu ndi zinthu za wamba zonse. Israyeli anali ndi Mulungu wa ngwiro.

Ciyero ca Mulungu cimakhudza za ubwino wace. Mulungu adacitira anthu ace zabwino. Mulungu wathu woyerayu adaonetsa cifundo kwa anthu ace pamene iwo adacimwa.

"Ciyero ca Mulungu" cidatanthauza kuti iye adakhala wokhulupirika ndi Israyeli. Iye adasunga malonjezano ace. Iye adawapatsa dziko limene adalilonjeza kwa Abrahamu, Isake ndi Yakobo. Mulungu wa Israyeli sanali kukonda zinthu zoipa. Iye sakadamalora anthu kuti adzicita cimo wopanda kulanga cimolo. Mulungu wao sadasamale pa zinthu zomwe zidapweteka anthu. Mulungu adawapatsa malamulo kuti asamabvutitsane wina ndi m'nzace.

Mulungu amafuna anthu ace kukhala monga Iye. Cimeneci cinali cobvuta kwa anthu a ci Hebri. Iwo anali kupembedza mafano ambiri pamene anali kukhala ku Aigupto. Mulungu ya Akenani idawayesa pamene anali mdziko la malonjezano. Kuli konse komwe anali kupita anali kuyesedwa kuti apembedze molinganiza ndi mwambo yacilendo. Iwo nthawi zonse anali kulephera.

Mulungu adakhazikitsa malamulo ace onse pa ciyero cace. Iye adapereka malamulo kuti anthu ace adziwe kuti iye anali wotani. Ngati iwo adakhulupirira mwa Mulungu amene "anali m'mwamba ndi wokwezedwa, adakayesa kumutumikira, cifukwa iye anali wosiyana. Iye anali ndi mphamvu ndipo anali woyera.

miyambo yao, ndi macitidwe ao osapembedza.

Pa maphunziro anai ena akubwerawa tikhala tiri kuyesa kuonetsa momwe tingakumanire ndi kukhala ndi cigonjetso pabvuto lakaleli: ndi momwe tingamakhalire monga Akristu mu dziko lamasiku ano osakhala monga anthu osakhulupirira omwe ali motizungulira.

Akristu samacipeza capafupi kukhala monga Kristu. Iwo amayesedwa kuti acimwe. Iwo amayesedwa kuti abise macimo ao. Koma Akristu ayenera kucita zinthu zimenezi mokondweretsa Mulungu. Iwo ayenera kukhala omvera pamaso pa Mulungu. Akristu sayenera kumaswa malamulo a Mulungu.

Anthu a Mulungu nthawi zonse akhala ngati anthu osadziwa Mulungu. Anthu anzao acikunja amawayesa kuti apembedza mafano. Iwo amapeza kuti kukhala miyoyo yabwino ndi cinthu cobvuta. Cimenecinsu ndi coonadi masiku ano.

Mulungu adapatsa malamulo anthu ace kuti adziwasunga. Buku la Levitiko ndi Buku la malamulo. Mulungu adafuna kuti Ahebri adzimvera malamulo ace. Mulungu adadziwa kuti anthu adasoweka malamulo wowathandiza kuti adzikhala miyoyo yoyera, ndi mtendere ndi Mulungu ndi anthu ena.

(Werengani Levitiko 19:1-4; 19:11-13; Yoswa 24:14-21 ku kalasi).

MULUNGU NDI WOYERA

Mulungu amayembekeza anthu ace kukhala oyera cifukwa iye ndi oyera. Kodi "ciyero ca Mulungu" cidatanthauza ciani kwa anthu a ku Israyeli?

PHUNZIRO 4

MPINGO NDI AULAMULIRO

MAU A MULUNGU OPHUNZIRIRA KUNYUMBA: Macitidwe 5:21-19; Aroma 13:1-10

MAU APHUNZIRO LALERO: Aroma 13:1-10

MAU APAMTIMA: "Ndipo anayankha Petro ndi atumwi, nati, 'Tiyenera kumvera Mulungu koposa anthu.'"

Macitidwe 5:29

M'maiko ena, anthu alibe ufulu wopembedza. Iwo amapembedza mtseri. Monga nzika za dziko lathu timakondwera ndi ufulu wa cipembedzo. Boma lathu limatilora ife kupembedza Mulungu monga momwe tifunira. Kodi tiri ndi nchito zotani zocitira dziko lathu? Kodi tikhoza kuphunzira ciani kucokera ku kalata ya Paulo ya mpingo wa kwa Aroma za nchito yathu ku dziko lathu? Ife tiri ndi nchito zina monga asanu wa Kodi ndi zotani?

Aroma anali kulamulira maiko ambiri m'masiku a Paulo. Boma la Aroma linali ndi zolinga zambiri zabwino. Linasunga Ayuda kuti asakhale pa nkondo. Linamanga miseu yabwino. Linali kuzenga Aroma onse akagwidwa ndi milandu.

Komabe Ayuda sanali kufuna kupereka msonkho wapamwamba kwa Aroma. Iwo sanafuna kuti dziko lina lidzawalamulire. Anafuna kudzilamulira okha.

Paulo pa ulendo wace wautumiki wacitatu, analemba kalata kwa Akristu aku Aroma. Timaphunzira ziphunzitso za Akristu kucokera ku kalata ya Paulo ya kwa Akristu. Akristu a ku

Aroma anadziwa za ndale ndi ulamuliro. Pamene iwo anakhala Akristu anayenera kudziwa momwe ziphunzitsa za Akristu zinanenera pa za maulamuliro.

Mu Aroma tiri kuphunzira za udindo wa Mkristu ku boma ndi mpingo. Mkristu ndi ciwalo ca mpingo ndi Boma. Iye ali ndi udindo okhala okhulupirika kwa onse. Paulo anali Mkristu okhulupirika. Iye anali kumvera lamulo la Aroma. Werengani pa ndime iyi. Kodi Paulo anati ciani?

(Werengani Aroma 13:1-10 kukalasi)

NCHITO YA AKRISTU KU BOMA

Ayuda sanali kukonda kumvera olamulira a ci Roma. Iwo anati Mulungu ndiye mfumu yao. Paulo anafuna kuti Akristu onse adzimvera olamulira a ci Roma ndi athandizi ace. Iye anachula anthu otere kuti "akapolo a Mulungu" (onani ndime 4).

Mkristu ayenera kumvera kapolo wa Mulungu. Mulungu anapatsa atsogoleri a boma mphamvu yao. Mulungu anawapatsa nchito kapena malo autumiki. Ngati munthu samvera boma, ali kukangana ndi malamulo a Mulungu. Ndiye kuti abweretsa ciweruzo pa iye yekha.

Anchito a lamulo sayenera kukhala oopedwa ndi iwo omvera lamulo. Akuru a malamulo amayamika amene amamvera lamulo. Iwo ndi akapolo a Mulungu. Iwo ali kugwira nchito yotithangatira. Koma ngati munthu acita zinthu zoipa, ayenera kuopa opatsa malamulo. Akhoza ndiponso adzamulanga.

Tiyenera kumvera opereka Malamulo pa zifukwa ziwiri. Mulungu adzaticwiira ngati

PHUNZIRO 10

ANTHU OYERA

NDIME ZOPHUNZIRIRA KUNYUMBA: Levitiko 19
Yoswa 24

NDIME ZA MPHUNZIRO LALERO: Levitiko 19:1-4
Levitiko 19:11-13
Yoswa 24:14-21

MAU APAMTIMA: "Koma ine, ndi a m'nyumba yanga, tidzatumikira Yehova."
Yoswa 24:15

Pali kufunitsitsa kwakukuru kufuna kubwerera ku "miyambo ya makolo." Pali mau odanda-ula m'dziko lonse la pansi kuti anthu asunge miyambo yao yakale; kuti asataye makhalidwe ao. Ndi cinthu ca bwino. Mtundu uli wonse uyenera kusunga miyambo ndi makhalidwe ao. Komabe mtundu uli wonse uli wofunika kuonetse-dwa pamaso pa Mulungu cifukwa ca momwe amatetezera ndi kusungira makhalidwe a mapembedzo ao cikhulupiriro cao mwa Mulungu ndi mapembedzedwe ao a kwa Mulungu. Anthu ena amafuna kulora miyambo yao kuwauza mtundu wa cipembedzo comwe ayenera kucita. Limeneli siganizo latsopano. Kapena kuti ndi ngozi yatsopano. Limeneli ndi yeso lomwe lakhala likuoneka zaka zambiri zapitazi.

Anthu a Mulungu a mu Cipangano ca Kale adayeseledwa kulola zikhulupiriro ndi miyambo ya ena, amene sanali opembedza a Mulungu, kupanga zikhulupiriro zao zao ndi njira zaka-khalidwe. Bvutoli ndi la kale ndipo lidakalipo masiku ao.

Kulapa mwa cikhulupiriro kwa Mulungu kuli kupitirizikabe pakati pa anthu akunja ndi

kupita kwa Iye. Funani madalitso a Mulungu lero pobvomereza ndikulapa macimo anu. Kodi mwaumirirabe ku macimo anu omwe adacokera kwa makolo anu? Motero cifukwa ciani? Mulungu adzakulangani. Ndi cinthu cabwino. kukhala okhululukidwa ndi kukhala ndi madalitso a Mulungu.

ZOMWE PHUNZIROLI LITIPHUNZITSA

1. Munthu amayesedwa kuti asiye Mulungu ndi kumapembedza mafano. Munthu amapembedza mphamvu, maudindo, cuma ca dziko ndi macimo a zilako lako. Mulungu sakondwa pamene munthu acita cimo.
2. Munthu asoweka atsogoleri amphamvu amene angalankhule motsutsana ndi cimo.
3. Cikhululukiro ca Mulungu pa macimo athu ndico ciyembekezo ca munthu. Munthu ayenera kulapa macimo ace ndi kutembenuka kuwasiya. Munthu ayenera kumvera Mulungu.

sitiwamvera iwo. Ndiponso cikumbu mtima cathu cidzamasuka ngati titawamvera.

Tiyenera kupereka misonkho yathu cifukwa ca cifukwa comweco. Pamene atsogoleri a boma atiuza kupereka mtengo wa msonkho, tiyenera kupereka. Anthu anchito yopanga malamulo ali kugwirira nchito Mulungu.

Paulo anati Akristu ayenera kupereka ku boma zomwe tiyenera kupereka. Tiyenera kuone-tsanso ulemu kwa ogwira nchito ya lamulo, ndi kuwalemekeza.

NCHITO YA MKRISTU KWA MUNTHU MNZACE

Tiyenera kubwezera ngongole kwa ena mwam-sanga monga tingathere. Sitiyenera kukhala ndi ngongole ndi wina aliyense. Paulo anati cikondi a pa Akristu ena ndico ciyenera kukhala ngongole. Mkristu aliyense amene amakonda ena amamvera malamulo a Mulungu.

Paulo analemba zambiri za malamulo a Mulungu. Iye anaika mndandanda asanu wa malamulo khumi. Malamulo asanuwa amakhudza za cimo la munthu ndi munthu wina. Mkristu sayenera kucita cigololo. Sayenera kupha kapena kuba. Mkristu sayenera kunena bodza lonena za mnzace kapena kufuna zimene ali nazo.

Werenganinso kumapeto a ndime 9. Kodi Mkristu akhoza kutsimikiza motani kuti sacita macimo oipa oterewa kwa munthu wina? Ngati iye akonda ena monga adzikondera iye mwini, adzamvera malamulo onse.

Mkristu sangacimwire wina aliyense amene amamukonda. Cikondi cimatenga malo a malamulo onse. Ngati tikonda ena, sitingacite kanthu

kowakhumudwitsa. Motero ngati tikonda ena, timamvera malamulo onse.

Kumvera kwathu koyamba kuyenera kupita kwa Mulungu. Iye ayenera kukhala oyambirira m'miyoyo yathu. Pamene tiri kuphunzira za Mulungu ndi zomwe amayembekeza kwa ife, timapeza maudindo ena a miyoyo yathu.

Mulungu amafuna kuti ife tidzimvera malamulo a dziko lathu. Iye amalora boma lathu kukhala ndi mphamvu kapena mwai wolamulira dziko.

Mulungu amayembekezera kuti ife tidzikonda ena. Ngati titero, sitidzawakhumudwitsa ndi mau kapena kutenga zinthu zao.

Kodi muli kukhala ndi makhalidwe amene Mulungu amayembekezera ife kuti tikhalire?

ZINTHU ZOYENERA KUGANIZA

Kodi timamvera malamulo a dziko lathu? Kodi timapereka misonkho yathu yomwe timayenera kupereka? Kodi tiri kumvera malamulo a Mulungu amene anatipatsa ife? Kodi timapereka cakhumi ca zonse zimene timazilandira? Kodi timakonda anthu ena monga timadzikondera eni tokha?

ZOMWE PHUNZIROLI LITIPHUNZITSA

1. Mulungu amapatsa mphamvu kwa atsogoleri a boma. Mphamvu imeneyi idayenera kuwathandiza kuweruza mwa nzeru ndi kugwira bwino nchito zao mwacilungamo. Iwo adzaweruzidwa ndi Mulungu ku nchito zomwe acita.
2. Mulungu amayembekeza Akristu kuti amvere malamulo a boma, kupatikiza kupereka misonkho.

Mose adapempha Mulungu kuti asaononge anthu ace. Iye adapempha Mulungu kuti akumbukire malonjezano ace akwa Abrahamu, Isaki ndi Yakobo. Werengani Pemphero la Mose la kwa Ahebri mu Eksodo 32:11-13. Mulungu adalanga anthu ace cifukwa ca macimo ao.

(Werengani Eksodo 32:35)

CIFUNDO CACIKURU CA MULUNGU

Mose adafuna kudziwa ngati Mulungu akondabe anthu ace. Iye adapempha Mulungu kuti awakhululukire. Ndipo Mose adakwiya cifukwa anthu adapanga mwana wa ng'ombe. Iye adaswa miyala ya malamulo pamene adaona kuti iwo ali kupembedza mwana wang'ombeyo. Mulungu adaitananso Mose kuti akwere phiri la Sinai. Adaperekanso malamulo khumi kwa Mose kaciwiri.

Mulungu adaika cizindikiro ca kupezeka kwace m'mitambo. Kodi Mulungu adanena ciani kwa Mose mu 34:6-7? (Muwerengerenso mu kalasi).

Mulungu adakali wokhulupirikabe ndi wacifundo kwa anthu ace. Iye amatikhululukira pamene tilapa macimo athu. Werengani I Yohane 1:9 kuphunzira momwe Mulungu angatikhululukirire. Mulungu amatikonda ife. Iye amatipatsa ife ufulu. Pamene ticimwa kulakwira Mulungu, tikhoza kulapa macimo athu. Iye adzatikhulukira ife.

ZINTHU ZOLINGALIRA

Kodi inu nthawi zina mumapembedza mafano? Kumbukani kuti Mulungu amaitana munthu aliyense kuti adziyankhire macimo ace. Mulungu ndi wacifundo. Iye adzatikhululukira ife. Iye amatsira madalitso ace pa ife tikabwerera

wa golidi. Pothera iwo anali ndi mulungu yemwe akadamuona.

MACIMO A ANTHU

Ahebri anali kupembedza fano la mwana wang'ombelo kunena kuti; "O Israyeli, uyu ndiye mulungu amene wakuturutsa iwe mu Aigupto!" Israyeli adacimwira Mulungu pamene iwo anali kupembedza fanolo. Werengani lamulo lomwe iwo adaliswa mu Eksodo 20:4-6.

Iwo adaphwanyanso lamulo la cisanu ndi ciwiri pamene iwo "adaimirira ndi kupemphera." Iwo adacita macitidwe a cigololo pamene adapembedza.

Mulungu adakhala wabwino kwa iwo. Ndi cifukwa ciani iwo adayenera kutembenuka nasiya Mulungu ndi kupembedza mafano? Ndi cifukwa ciani adaiwa mwa msanga motere?

MULUNGU ADAKWIYA

Mulungu adakwiya. Mulungu adadziwa kuti anthu ace adatembenukira ku mafano. Iye adauza Mose kuti atsike ndikupita pansi ndi kukaona zomwe anali kucita. Ahebri adatembenuka kusiya Mulungu. Iwo adaswa lonjezano lao la kwa Mulungu. Iwo anali wosakhulupirika.

Ife sitingathe kukondweretsa Mulungu ngati tikupembedza mafano. Mulungu ayenera kukhala oyamba mu miyoyo yathu. Werengani zomwe Yesu adauza mnyamata wina mu Mateyu 22:37-38.

Mulungu sakadakhocha kungosiya mapembedzedwe a mafano a Ahebri. Iwo adayenera kulangidwa. Mulungu adafuna kuwaononga iwo.

3. Mulungu amayembekeza kuti ife tidzisunga malamulo ace.
4. Mulungu amayembekezera kuti ife tidzilemekeza maudindo a anzathu.
5. Mulungu amayembekeza kuti tidzikondana wina ndi mnzace monga momwe timadzikondera tokha. Ngati tikondana wina ndi mnzace sitidzafuna kukhumudwitsa wina. Sitidzafuna kutenga zomwe ziri za wina.

PHUNZIRO 5

KULILIRA UFULU

MAU A MULUNGU OWAPHUNZIRIRA KUNYUMBA: Eksodo 1-2

MAU A MULUNGU A PHUNZIRO LALERO: Eksodo 1:7-14,22; Eksodo 2:23-25

MAU APAMTIMA: "Idzani kuno kwa Ine nonsenu akulema ndi akuthodwa, ndipo Ine ndidzakupulumutsani inu, senzani gori langa, ndipo phunzirani kwa Ine, cifukwa ndiri wofatsa ndi wodzicepetsa mtima; ndipo mudzapeza mpumulo wa miyoyo yanu. Pakuti gori langa liri lofewa, ndi katundu wanga ali wo pepuka."

Mateyu 11:28-30

Dziko liri lonse likufuna kukhala laufulu. Akufuna kukhala afulu kuti adzilamulira okha dziko lao, kupanga okha malamulo ao ndi kudzi-sankhira okha atsogoleri ao.

Ufulu umodzi wofunika koposa ndi ufulu wopembedza Mulungu monga momwe tifunira. Mulungu anaitana Abrahamu kuti ayambe mtundu

watsopano. Iye anafuna anthu ace adzimupembenda Iye. Mwana wa Abrahamu Isaki ndi mdzukululu wa Yakobo anali kukhala mdziko latsopano. Pamene Yakobo anali okalamba, nthawi yobvuta inabwera. Mvula siinabwere ndipo panalibe cakudya comwe cinamera. Njala yaikulu inabwera pa dziko lonse. Yakobo anatumiza ana ace kuti apite ku Aigupto kukafuna cakudya. Iwo anapeza cakudya ndi malo okhalapo. Werengani zomwe zinaoneka kwa iwo.

(Werengani Eksodo 1:7-14;22 mukalasi)

FARAO WATSOPANO

Banja la Yakobo linapita ku Aigupto kukhala. Farao kapena mfumu inali yacifundo kwa Yakobo ndi ana ace. Patapita zaka zambiri, Yakobo ndi ana ace anafa. Farao wina anali kulamulira Aigupto. Farao ameneyu sanali wa cifundo kwa Ahebri.

Farao anaopsa a Hebri. Mulungu anacurukitsa ciwerengero ca Ahebri. Farao anali kuopa kuti adzayamba kumulamulira ndikulanda boma lace. Farao anaganiza kuti Adani ocokera ku mpoto adakakhoza kutsira nkondo ku Aigupto, Ahebri akadathandiza kuti amenye Aigupto. Motero Farao anaganiza njira zobvutitsira anthu a Mulungu. Iye anaganiza njira yocetsetsera kaculukidwe ka Ahebri.

FARAO ANACULUKITSA KATUNDU WAO

Farao anapanga Ahebri kukhala akapolo. Akuru anchito a Farao anansenzetsa Ahebri akatundu olemera.

Farao anali kuwamangitsa "mizinda yosungiramo cuma" kapena "yosungiramo zakudya."

MOSE AKOMANA NDI MULUNGU

Mose adakwera pa phiri la Sinai. Iye adamvera kwa Mulungu. Mulungu adapereka malamulo ambiri kwa anthu ace. Iye adauza Mose momwe akadapangira likasa. Mose adakhala pa phiripo kwa masiku makumi anai ndi usiku wace.

Ahebri sanakondwere. Cikhulupiriro cao cinafooka. Iwo anasiidwa ku nthawi yaitali. Ahebri anaganiza kuti Mose sadzabweranso. Iwo adafuna wina wace kuwauza zocita. Iwo adasoweke utsogoleri ndi cithandizo. Aroni sanali mtsogoleri wao. Aroni anali wolankhulira Mose. Iye adaiwalanso Mulungu.

Ahebri adafuna Mulungu amene akadamuona kuti awatsogolere. Iwo adapempha Aroni kuti awapangire mulungu ofanana ndi amene adamuona ku Aigupto.

ARONI ADATAYA CIKHULUPIRIRO: MTSOGOLERO WOFOKA

Kulimba mtima kwa Aroni kunafooka. Iye anali wofooka. Iye sanathe kuletsa anthu kuti asatumikire milungu ina. Iye adafuna kuwako-ndweretsa iwo. Iye adaiwala Mulungu. Iye adafuna malo ndi mphamvu yokhala mtsogoleri wao.

Ahebri adatopa kukhala ali kudikira Mose. Iwo anali kudabwa cifukwa cimene Mulungu adamusungira kwa nthawi yaitali. Motero Ahebri anakhala olimba mu cikhulupiriro cao. Ambiri sanathe kutero. Adatembenuka motsutsana ndi Mulungu.

Aroni adapempha anthu kuti amupatse ndolo zao za golidi. Iye adatenga golidi ndi-kumuyenga. Iye adapanga mwana wa ng'ombe

tsopano iye amakhulupirira Mulungu.

Ahebri adalonjeza kwa Mulungu ndi malamulo ace, koma posacedwa iwo adaiwala. Iwo sadakwa-niritsidwe. Iwo adakumbukira mafano ambiri a Aigupto ndi milungu. Iwo adaganizira zotembe-nuka kufulatira Mulungu. Adayamba kuonetsa kusakhulupirika kwao.

Koma Mulungu anakhalabe wokhulupirika!

Iye anakhala okhulupirikabe kwa Ahebri. Iye adamva kulira kwao pamene anali akapolo mu Aigupto. Iye adakumbukira lonjezano lace la kwa Yakobo ndi Yosefe.

Mulungu adaitana atsogoleri kuti atsogole-re Ahebri poturuka mu Aigupto. Iye adapatsa Mose ndi Aroni kulimba mtima kuti akaonane ndi Farao.

Aigupto adayesa kusunga Ahebri mu Aigupto. Koma Mulungu adatumiza milili khumi. Motero Farao adawalora kuti apite. Ahebri adaoloka Nyanja yofiira pamene Mulungu adagawa madzi pakati. Iwo adalandira malamulo khumi pa phiri la Sinai. Pambuyo pace Aisrayeli adakhala mtundu wotsogozedwa ndi Mulungu.

Mulungu adacitira anthu ace zinthu zambiri. Kodi iwo nthawi zonse anali kukonda ndi kutumikira Iye? Ai. Koma Mulungu anakhalabe okhulupirika kwa iwo. Iwo sanali wokhulupirika kwa Mulungu, koma Mulungu adawakondabe ngakhale adacimwa. Werengani ndime izi za cikondi ca Mulungu.

(Werengani Eksodo 32:1-6; 9-10; Eksodo 34:1, 6-7 ku kalasi).

Mizinda imeneyi inali kumangidwa ndi njerwa za 18" muyeso wace. Ahebri anagwira nchito molimba pomanga njerwazo. Koma anali kuculukirabe ngakhale anali ndi nchito yolimba.

Ndipo Aigupto anaonjezera magwiridwe a nchito a Ahebri ndi kuwaonjezera nthawi. Iwo anali kuwanyamulitsa akatundu a akuru a njerwa ndi matope. Akapitao ankhanza anawalamulira mopanda cifundo. Komabe Ahebri anaculukabe ciwerengero cao.

Ndime 15-21 ili kuti uza za njira ina imene Farao analangira Ahebri. Tsiku lina analamulira kuti ana onse acimuna a Ahebri adziponyedwa mu mtsinje wa Nile. Iye anaganiza kuti macitidwe otere akhoza kuletsa maculukidwe a Ahebri.

(Werengani Eksodo 2:1-9 mukalasi)

MULUNGU APEREKA MTSOGOLERI KWA AHEBRI

Mwana wamwamuna anabadwa kwa atate ndi amai a ci Hebri. Iwo sanafune kumuponya mu mtsinje wa Nile. Motero anamubisa iye ku nyumba kwa miyezi itatu. Pamene mai wace sakana-khoza kumubisanso, anapanga kadengu kakang'ono. Anakapaka utoto kuti madzi asalowe mkati. Ndipo anaika mwana wace mkatimo. Ndikuyandamitsa kadenguko pa m'tsinje pakati pa mabango. Amai a mnyamatayo anali ndi cikhulupiriro kuti Mulungu adzapulumutsa mwana wace. Mlongo wace anali kumudikirira.

Mwana wa mkazi wa Farao anapeza mwanayo. Iye anamva cifundo naye. Mlongo wa Mose anamuza kuti amupezere olela mwanayo. Iye anapeza mai wace. Mai a Mose analandira ndalama pomwe anali kusamala mwana wace! Iye anauza Mose za

Mulungu. Iye anamuuza za Abrahamu, Isaki ndi Yakobo. Mulungu anamugwiritsa nchito yophunzitsa mwana wace kuti adzatsogolere anthu ace.

Mose anaphunzitsidwa monga mwana wa mfumu. Koma iye anakondabe anthu a mtundu wace. (Werengani Ahebri 11:24-25) Tsiku lina Mose anaona munthu wa mu Aigupto akumenya munthu wa ci Hebri. Mose anapha munthu wa ci Aigupto ndikuthawa kucoka m'dzikomo, cifukwa Farao anafuna kupha Mose.

ANALIRIRA THANDIZO

Ukapolo wa Ahebri unakula kwambiri ndiku-
ipa koposa pamene Mose anali kunja kwa dzikolo.
Katundu wao unali wolemera kwambiri osatheka
kumunyamula. Ndipo anakumbukira Mulungu wao.
Iwo anapempha cithandizo.

Mulungu anadziwa za anthu ace. Iye anakumbukira malonjezo ace a kwa makolo ao. Iye anamvera kulira kwao. Mulungu anadziwa nthawi inafika yacipulumutso cao. Mulungu anali okonzeka kupatsa anthu ace ufulu. Ahebri anayambanso kupemphera kwa Mulungu.

ZINTHU ZOLINGALIRA

Kodi mumaona kuti mumanyamula akatundu olemera? Kodi mukutaya kulimba mtima kwanu? Mulungu amadziwa za akatundu anu. Iye anapanga njira yokupatsani ufulu kucoka ku akatundu anu. Werengani Mateyu 11:28-30. Musaleke kupemphera kwa Mulungu kuti akupatseni mpumulo. Mulungu adzakupatsani mphamvu ya tsiku ndi tsiku. Pemphani cithandizo.

PHUNZIRO 9

ANTHU OSAKHULUPIRIKA - MULUNGU WOKHULUPIRIKA

NDIME ZOPHUNZIRIRA KUNYUMBA: Eksodo 32:1-34:9

NDIME ZA MPHUNZIRO LALERO: Eksodo 32:1-6;9-10
Eksodo 34:1;6-7

MAU APAMTIMA: "Ndipo Yehova anati kwa Mose, 'Iye amene wandicimwira, ndifafaniza yemweyo kumcotsa m'buku langa... Ine ndidzawanga langa cifukwa ca kucimwa kwao."
Eksodo 32:33,34

Palibe kanthu kuti kaya munthu apita kuti kapena kuti alandira maphunziro otani, iye sataya cikoka cace ca kale. Munthu amatenga makhalidwe abwino ndi oipa kucokera kwa makolo ace. Cifukwa cakuti tonse ndife zidzukululu za Adamu, tidzapitiriza kupanga zolakwa. Koma Mulungu adatipatsa njira yogonjetsera zolakwazi ndi macitidwe ocimwa. Kupyolera m'mwazi ndi cikhululukiro mwa Yesu, tikhoza kukhala ndi cigonjetso ca cimo ndi Satana m'miyoyo yathu.

Bwenzi la ci Africa adanena momwe anali kukhalira pofuna kuyambitsa mabvuto, kuba, ndi kumenyana. Tsiku liri lonse anali kumapita kunja kwa nyumba yace ndikukaona ngati wina ali kukangana anali kupita ndi kukakangana nawo.

Iye anali kukonda kucita ndeu. Tsiku lina, adafika pozindikira cikondi ca Mulungu. Iye adalandira cikhululukiro ca zolakwa zambiri mbiri zomwe adacita. Iye adasanduka kukhala munthu wa mtendere ndi wacikondi. Iye adaona mphamvu ya cisomo ca Mulungu. Iye adati adayenera kulangidwa, koma Mulungu adamukhulukira. Iye anali cilengedwe ca tsopano mwa Yesu. Iye adakhala ali wosakhulupirika;

Mulungu amadalitsa maiko athu pamene tikuyesa kukhala mowatsata.

Kodi inu mumapempherera dziko lanu ndi atsogoleri ace? Ngati ife timvera Mulungu, tidzakhala anthu abwino. Tidzamvera malamulo ace ndi malamulo adziko lathu.

ZINTHU ZOLINGALIRA

Malamulo khumi a Mulungu! Mulungu adawapereka kwa ifenso. Kodi timayesa kuwasunga? Kodi timayesa kukhala ndi njira ya miyoyo yokondweretsa Mulungu?

ZOMWE PHUNZIROLI LITIPHUNZITSA

1. Mulungu amagwiritsa anthu kuti apange mtundu waufulu.
2. Mulungu adagwiritsa nchito anthu omweo kuti athandize kupitiriza dongosolo lace ndi cifuniro cace ca mtundu watsopanowo.
3. Anthu ayenera kukhala ndi malamulo owasunga. Mau a Mulungu amapereka utsogoleri kwa anthu amene ali a Mulungu.
4. Mulungu amadalitsa mtundu omwe anthu ace amamumvera.

ZOMWE PHUNZIROLI LITIPHUNZITSA

1. Paciyambi Mulungu anapanga anthu afulu.
2. Anthu anasankha kufulatira Mulungu potsata njira yao ndi kuiwala Mulungu.
3. Ambiri ndi opweteka cifukwa siali afulu kumakhalidwe ao aucimo.
4. Anthu ambiri ndi opweteka cifukwa ca akatundu olemera amene amawanyamula cifukwa ca makalidwe aucimo ndi zokhumba zodzikonda za ena.
5. Mulungu amakonda anthu onse. Iye amafuna onse kukhala afulu - afulu kuucimo ndi afulu kucoka ku zolemetsa.
6. Mulungu amafuna Akristu kukhala okonzeka kuthandiza anthu amene anyamula katundu olemera.

PHUNZIRO 6

AITANIDWA KUTSOGOLERA

MAU A MULUNGU OPHUNZIRIRA KUNYUMBA: Eksodo 3-4

MAU A MULUNGU APHUNZIRO LALERO: Eksodo 3:3-15
Eksodo 4:10-16

MAU APAMTIMA: "Pakuti mphatso zace ndi kuitana kwace
kwa Mulungu sizilapika."
Aroma 11:29

Mnyamata wina sanakwaniritsidwa kunyumba. Iye sanakhoze kupeza nchito. Iye anaganizira zocoka kumudzi kwao. Iye anapita ku mzinda wakutali. Iye anakhulupirira mwa Yesu ali mu mzinda umenewo. Patapita kanthawi pang'ono, anadziwa kuti Mulungu ali kumuitana kuti akhale mbusa. Iye anabwerera kumudzi wace. Kunalibe malo otumikira ubusa. Iye anapita kumudzi ndi-kutsogolera abale ace kwa Kristu. Ndipo Mulungu anatsegula khomo lakuti akhale mbusa. Iye anatumikira ubusa kwa zaka zisanu ndi cimodzi. Ndipo anapita ku sukulu ya ubusa. Aphunzitsi asukulu ya ubusa anayesa kumuphunzitsa iye kukhala olalikira pa cipatala. Iye anati, "Ai, Mulungu anandiitana kuti ndikhale mbusa." Iye anafunsidwa kuti acitire Yesu zinthu zina zinthu zabwino, koma nthawi zonse anali kuyankha kuti, "Mulungu anandiitana kuti ndikhale mbusa." Iye adakali mbusa ndipo Mulungu ali kudalitsa nchito ya munthu ameneyu cifukwa anamvera kuitana kwa Mulungu kuti akhale mbusa. Iye anabvomera kutsata dongosolo la Mulungu la moyo wace. Zoonadi Mulungu amaitana anthu kuti amutumikire.

Kulira kwa anthu a ci Hebri kunafikira Mulungu. Mulungu anayamba kugwira nchito ya

kodi adacita zonse zimene adalonjeza?

Kodi inu mumacita malonjezano kwa Mulungu? Kodi ndikoyenera kucita malonjezo ngati simu-ngathe kuwasunga?

MALAMULO KHUMI

Werengani malamulo khumi kucokera mu Buku Lopatulika lanu - Eksodo 20:1-17. Malamulo ena omwe Mulungu adapatsa Ahebri adalembedwa mu Eksodo 21 ndi 22.

Mose adauza anthu malamulo onse macitidwe onse amene Ambuye adamupatsa. (Werengani Eksodo 24:3) Anthu anali ndi malamulo a Mulungu owasunga. Malamulo amenewa ndi osatha. Ndipo nthawi zonse ndi abwino ndi olungama.

Ahebri adapanga pangano ndi Mulungu. Iwo adayenera kukhala anthu a Mulungu. Iwo adayera kumumvera Iye. Mose ndi Ahebri adasonkhana pa phiri la Sinai kubvomereza pangano.

MOSE APANGA GUWA LA NSEMBE

Mose adagwiritsa nchito miyala khumi ndi iwiri pa guwa la nsembepo, umodzi wa kuimira mtundu uli wonse wa Aisrayeli. Ahebri adape-mbedza Mulungu popereka ana a ziweto pa guwapo. Mwazi wa nsembeyo udathandiza kuwakumbutsa pangano lomwe adacita ndi Mulungu. Iwo anali kuonetsa Mulungu kufuna kwao kwa kukhala anthu ace. Iwo adafuna kumvera Mulungu.

Malamulo ambiri a mitundu yathu ndi mau-fulu adacokera mu Buku Lopatulika. Buku Lopatulika ndilo maziko a malamulo amene ali kulamulira mitundu yambiri masiku ano. Malamulo amathandiza kutsogolera ife, ndipo

anali kuyenda ku Sinai.

Ahebri adasoweka citsogozo ca Mulungu. Iye adawabweretsa ku Sinai kuti akalandire malamulo ace. Iye adafuna anthu ace kudziwa kuti alinao.

MALONJEZO A MULUNGU

Mose adamvetsera kwa Mulungu pa phiri la Sinai. Mulungu adapereka pangano kwa iye. Pangano ndi cimvano ca pakati pa anthu awiri kapena ambiri. Pano cikutanthauza pangano la pakati pa Mulungu ndi anthu ace. Kodi Mulungu adalonjeza ciani? Werengani Eksodo 19:5-6 kaciwiri.

Ahebri adayenera kukhala anthu a padera opatulikira Mulungu. Ngati iwo adzasunga malamulo ace, adzakhala anthu ace apadera.

Mulungu adafuna kuti iwo akhale mtundu wa ufumu wa ansembe. Iye adawaitana kuti akhale mtundu woyera. Iye adawapatula kucoka ku mitundu ina. Mulungu adacitira Ahebri zinthu zabwino zokondera pamene adawacha anthu ace.

Mulungu amagwirabe nchito ndi mitundu ya anthu. Iye amafuna kuti adzicita cifuniro cace. Mulungu amagwira nchito kupyolera mwa atsogoleri a mtunduwo.

Mose adatsika kucokera pa phiri la Sinai. Iye adaitana atsogoleri a Ahebri kuti akumane naye, ndi kuwauza za malonjezo a Mulungu.

KUYANKHA KWA AHEBRI

Werenganinso 19:8. Anthu adalonjeza kumvera Mulungu. Iwo adapanga malonjezo abwino. Iwo adakhulupirira kuti akhoza kumvera Mulungu. Pamene zaka zidapita pang'ono,

dongosolo lowapulumutsa. Kudatenga zaka makhumi asani ndi zitatu kuti Mulungu akonze Mose kugwira nchito imene anafuna kuti amucitire.

Werengani momwe Mulungu anaitanira Mose kuti atsogolere anthu a Mulungu kuturuka mu Aigupto.

(Werengani Eksodo 3:3-12 kukalasi)

MULUNGU ANAITANA MTSOGOLERI WA ANTHU ACE

Mose anakhala ku Midiyani kwa zaka zambiri. Iye anali kusamalira nkhoa za Jetero. Iye anakwatira mwana wa mkazi wa Jetero. Tsiku lina Mose anatenga nkhoa zace ndikupita ku Horebi. Anthu anali kucha Horebi kuti "ndi phili la Mulungu."

Abusa anali ndi nthawi yoganizira. Mose anaganizira za anthu ace mu Aigupto. Iye anakumbukira momwe anali kubvutikira.

Pamene Mose anali kuyenda pa Phiri la Horebi, anaona cozizwitsa! Mose anaona maonekedwe atsopano. Iye anaona citsamba ciri kuyaka moto - citsamba comwe sicinanyeke! Mulungu anaitana kuti, "Mose, Mose," Mose anati "ndiri pano." Mulungu anaitana Mose pochula dzina lace! Mulungu amadziwa maina athu onse. Mulungu amadziwa aliyense pa yekha.

Mulungu anauza Mose zinthu zitatu. "Waimapo ndi malo opatulika. Bvula nsapato zako." Mose anaima pamaso a Mulungu. Kaciwiri Mulungu anati, "Ine ndine Mulungu wa makolo ako Mulungu wa Abrahamu, Isaki, ndi Yakobo." Mose anadziwa kuti Mulungu ali kulankhula. Motero anaphimba nkhope yace ndi manja ace. Mulungu anati anadziwa kuti anthu ace anali kubvutika. Iye adayenera kuwapulumutsa

kucokera ku Aigupto. Anayenera kuwatsogolera ku dziko la malonjezano.

Kodi Mose anali okonzeka kukhala mtsogoleri? Werengani ndime 10-11 kukalasi. Koma Mose anati kwa Mulungu, "kodi ine ndine yani kuti ndipite kwa Farao, ndikuti ndikaturutse ana a Israyeli kucokera mu Aigupto?"

(Werengani Eksodo 3:12-15 kukalasi)

KUPITA MOSAKONDWA

Mulungu anakonzeka kutumiza Mose kwa Farao. Inali nchito yolimba. Mose anakumbukira cifukwa cimene anacokera ku Aigupto. Kodi iye akadabwerera ndikukakhala ndi moyo? Mose anaganiza kuti nchitoyo inali yaikuru kwa iye. Iye anati sakanakhoza kulankhula. Iye anapereka zowilingula kwa Mulungu kuyesa kugonjetsa Mulungu kuti asankhule wina wace. Mose anafuna kudziwa dzina la Mulungu amene anamuitana. Ahebri amakonda kufuna kudziwa dzina la Mulungu. Mulungu aliyense mu Aigupto ali ndi dzina. Anthu anali kuitana milungu yao maina pamene anali kupempha thandizo. Mulungu anauza Mose dzina lace. Dzina la Mulungu linatanthauza kuti anali kukhala pakati pa anthu ace. Mulungu analonjeza kuti adzakhala ndi Mose monga momwe anakhalira ndi makolo ace. Koma Mose anali ndi mantha kuti apite ku Aigupto.

Werengani ndime izi kuti mupeze momwe Mulungu anayankhira Mose.

(Werengani Eksodo 4:10-16 mu kalasi)

MULUNGU ANALONJEZA KUTHANDIZA

Mulungu anauza Mose kuti ndiye anapanga pakamwa. Iye akadayenera kuthandiza Mose

Mulungu adawapulumutsa iwo kucokera ku Aigupto. Ndipo zinthu zambiri zidaoneka zomwe zidawapanga kukhala osakondwa. Iwo adaganiza kuti adzabvutika. Mulungu adawapatsa mana ndi dzinziri kuti adye. Iwo analibe madzi. Mose adamenya mwala ndipo madzi adatuluka. Iwo adamenyana ndi Amaleki. Mulungu adawathandiza kuti apambane.

Mulungu adathandiza Ahebri mu njira zambiri. Iwo anasowekabe thandizo lace. Iwo adasoweka malamulo owatsata. Anthu adasoweka malamulo pamene anali kukhala pamodzi. Eksodo 19-20 ndi 24 amafotokoza za malamulo a Mulungu. Malamulo amenewa adathandiza Ahebri kuti akhale mtundu. Pezani malamulo mu ndime izi.

(Werengani Eksodo 19:3-8; 24:3-8 mu kalasi)

PA PHIRI LA SINAI

Ahebri atangooloka nyanja yofiika, Mose adawatsogolera ku Phiri la Sinai. Iwo adaika cigono pa mbali pa phiri pomwe anali kudikirira Mulungu kuti awapatse malamulo.

Mose adakwera Phiri la Sinai kukakomana ndi Mulungu. Iye adayembekezera Mulungu kuti alankhule naye.

UTHENGA WA MULUNGU KWA AHEBRI

Mulungu adapatsa Mose uthenga wa kwa anthu ace. Iye adafuna kukumbukira zomwe adawacitira. Mulungu adacita zinthu zimenezi kuti apange mtundu wa anthu mwa Ahebri.

Mulungu adauza Mose kuti Iye adanyamula Aisrayeli pa mapiko a mphungu. Iye adapulumutsa Ahebri monga adakwera pa mapiko a mphungu. Iye adawasunga mwaufulu pamene anali kuoloka nyanja yofiira. Iye anali kuwasamalira pamene

PHUNZIRO 8

MUNTHU UPEMBEDZA MULUNGU

NDIME ZOPHUNZIRIRA KUNYUMBA: Eksodo 19-20;24

NDIME ZA MPHUNZIRO LALERO: Eksodo 19:3-8;
Eksodo 24:3-8

MAU APAMTIMA: "Usakhale nayo milungu yina koma Ine ndekha, Usadzipangire iwe wekha fano losema,...usazipembedze izo, usazitumikire izo."

Eksodo 20:3-5

Pamene Amwenye adauzidwa kucoka ku Uganda zaka zapitazo, banja limodzi lidapita ku America. Iwo anali ndi abwenzi omwe anali Akristu ndipo anali a Baptist. Anthu a Baptist, omwe anali mu mzindamo adawathandiza kuti apeze malo okhala ndi kupeza nchito. Banja la cimwenyelo lidayamba kupita kumisonkhano. Tsiku lina onsewo adabvomereza Yesu monga Mpulumutsi wao. Iwo adayamba kumacitira umboni kwa ena. Iwo adati, "kodi ife tidakhala akhungu motere cifukwa ciani? Ndi cifukwa ciani tinali kupembedza mafano amenewo? Kunali kulakwa kwakukuru! Tiri kuthokoza Mulungu wati-khululukira!"

Mulungu amafuna anthu kumupembedza Iye. Iye amafuna mitundu ya anthu kumuzindikira iye monga Mulungu, ndi kuzindikira mphamvu yace. Iye amafuna anthu onse kuti amupembedze iye.

Anthu ambiri mu dziko lathu lero alibe ufulu wopembedzera Mulungu. Nthawi zina cimatenza zaka zambiri mtundu wa anthu usanapereke ufulu umenewu.

Ahebri naonso adatenga zaka zambiri kuti achedwe mtundu. Iwo anali okondwa pamene

polankhula. Mulungu akadaphunzitsa Mose zoyenera kunena. Mose anayesabe kuturuka muutumi-ki wa Mulungu.

Mulungu anakalipa kwambiri cifukwa ca Mose. Iye sanakondwere ndi zowiringula za Mose. Mulungu anaitana Mose kuti atsogolere anthu ace kuwatulutsa mu Aigupto. Ndipo Mose anafunsa mthandizi. Mulungu anati, "mbale wako Aroni ndiye munthu wolankhula bwino. Iye ali kukufunafuna tsopano. Adzalankhula m'malo mwako."

Tsopano Mose analibe zowiringula. Mulungu anamuthandiza poyankha dandaulo liri lonse analipereka. Mose anaganizira zomvera Mulungu.

Iye analankhula kwa Jetero, mpongozi wace, zobwereranso ku Aigupto. Iye anauza Mose kuti apite mu mtendere.

Mose anayamba kubwerera kupita ku Aigupto ali ndi mkazi wace ndi ana. Aroni anakumana naye asanafike ku Aigupto. Mose ndi mbale wace, Aroni anaitanidwa kuti atsogolere Ahebri kuturuka mu Aigupito.

Mulungu atangoitana Mose ndi Aroni, analonjeza kuti adzawathandiza. Iye anawapatsa mphamvu yotumikira. Pamene Mulungu aitana munthu, amawapatsa mphamvu yotumikira nayo.

Davide anakhala Mkristu. Iye sanaganize kuti adakacitira zambiri Mulungu. Tsiku lina mbusa wace anamupempha kuti akonze malo a mpingo. Ndipo nthawi zina anayamba kuphunzitsa ana. Ndipo anayamba kutsogolera nyimbo za mu mpingo. Davide sanawilingule kuti asatumikire Mulungu ndi mpingo. Iye anagwiritsa matalenti ace kutumikira Mulungu.

Aliyense akhoza kupeza zowilingula. Mukhoza kupeza zowilingula nthawi ili yonse yomwe Mulungu akukufunani kuti mumutumikire. Ganizirani za zowiringula zomwe mumazona apa ndi apo. Musagwiritse nchito cowiringula kuti musatumikire mpingo. Lolani Mulungu kuti akuthandizeni kucita nchito ya mpingo. Mulungu anathandiza Mose ndipo alikufuna kukuthandizani.

ZINTHU ZOYENERA KUGANIZIRA

Pamene Mulungu alankhula kwa ife, kodi timamumva? Mulungu amalankhula kupyolera anthu a Mulungu, monga azibusa, akuru a mpingo, Akristu ena. Kodi timapereka zowilingula zofooka pamene tafunsidwa kuthandiza nchito ya Mulungu? Kodi zowilingulazo ndi zobvomerezeka pamaso pa Mulungu? Mulungu amaitana atsogoleri kuti amutumikire. Kodi inu ndinu mtsogoleri amene Mulungu alikumuitana?

ZOMWE PHUNZIROLI LITIPHUNZITSA

1. Mulungu amafuna kunyamula akatundu amene tili kuwanyamula, koma ifeyo tiyenera kumulora.
2. Mulungu amaitana anthu kuti atsogolere anthu ace kuti akule mwa uzimu. Iye amaitana anthu kuti atsogolere ena kwa Mulungu.
3. Anthu ambiri amakhala ndi zowilingula zopatsa Mulungu zowaletsa kuti asacite nchito ya Mulungu.
4. Mulungu sangaitane wina wace ku mutumikira, osamupatsa njira yakatumikiridwe. Ngati Mulungu aitana, amapatsanso luntha lamatumikiridwe.

ZINTHU ZOLINGALIRA

Kodi muli ndi katundu wamkuru amene muli kunyamula? Kodi muli kufuna kuti Mulungu akupulumutseni kuzimenezo? Kodi muli kufuna thandizo la Mulungu? Ahebri adayenera kumvera Mulungu, m'malo mofuna kukhala afulu. Kodi inu muli ndi cikhulupiriro mwa Mulungu?

ZOMWE PHUNZIROLI LITIPHUNZITSA

1. Mulungu amathandiza anthu ace mu nthawi ya mabvuto ndi yosowa.
2. Mulungu amapatsa atsogoleri kutsogolera anthu ngakhale mtundu wa anthu kukhala afulu - ufulu kucokera ku ucimo ndi kucokera koponderezedwa.
3. Satana adzagwiritsa nchito aliyense kufuna kulepheretsa cifuniro ca Mulungu kuti cisacitike.
4. Mulungu sadzagonjetsedwa. Cifuniro cace cidzakwaniritsidwa.
5. Pempherani kuti Mulungu adzatsogolera ndi kuthandiza atsogoleri athu kuti akhale atsogoleri abwino kuti mtundu wathu udali-tsidwe ndi kutsogoledwa ndi Mulungu kuti ukhale ndi mtendere ndi cuma.

woipa koposa unzace. Miriri isanu ndi inai inali yoipa koposa zinthu zambiri zoipa zomwe zidaoneka pa caka. Farao adalonjeza kumasula anthu muriri uli wonse ukatha. Akatero "anali kulimbitsa mtima wace," ndipo anali kupitanso ku malonjezo ace. Tikhoza kuwerenga za miriri mu Eksodo 7-9.

Mose adacenjeza Ahebri za muriri wa khumi. Mabanja a Cihebri adakonzekera kuti adzipita. Iwo adapaka mwazi pa mphuthu za makomo ao. M'ngelo wa imfa adapitirira nyumba zao monga momwe Mulungu adawauzira.

Aigupto sadaike mwazi pa mphuthu za nyumba zao. Mngelo wa imfa adaima pa zitseko zao ndipo mwana woyamba kubadwa ali yense wa Aigupto adamwalira. Ndiponso ciweto coyamba kubadwa ca ziweto zao zidafa. Anthu aku Aigupto adafuna kuti Ahebri apite. Aigupto adaopa Mulungu kuti angaphe anthu onse (Werengani Eksodo 12:30-33).

MULUNGU ADAPULUMUTSA AHEBRI

Mulungu adamasula Ahebri kucokera ku Aigupto ndi ukapolo. Iye adawapatsa atsogoleri. Iye adapweteka Aigupto. Anthu a Mulungu sadaiwale ciombolo cao. Caka ndi caka kuyambira nthawi imeneyo, Ahebri amakondwerera phwando la Paska, kukumbukira momwe Mulungu adawapulumsira iwo.

Pali nyimbo imene imanena kuti, "Khalani ndi cikhulupiriro mwa Mulungu, Iye amasamalira anthu ace." Ahebri anali ndi cikhulupiriro. Kodi mumakhulupirira kuti Mulungu amatithandiza masiku ano? Kodi iye akhoza kukuthandizani motani? Pemphani cikhulupiriro cacikuru kwa Mulungu.

5. Tiyenera kukhulupirira Mulungu kotheratu, pamene Iye atiitana ife. Iye adzatithandiza kuti ticite nchito yomwe watiitanira kuicita. Mulungu ndi okhulupirika.

PHUNZIRO 7

MULUNGU MTHANDIZI WATHU

MAU A MULUNGU OWAPHUNZIRIRA KUNYUMBA: Eksodo 5 kufikira pa 14

MAU A MULUNGU APHUNZIRO LALERO: Eksodo 5:1-8; Eksodo 12:29-34

MAU APAMTIMA: "Pakuti Ine Yehova Mulungu wako ndidzawgwira dzanja lako lamanja, ndi kunena kwa iwe, Usaope ndidzakuthandiza iwe."
Yesaya 41:13

Anthu ambiri (asilikali) anakhala akaidi pa nthawi ya nkhondo ku Vietnam. Ena mwa akaidiwo anali Akristu. Atangomasulidwa, ndi kubwerera kumudzi, ena anali kufotokoza momwe Mulungu anawathandizira pamene anali ku ukapolo. Munthu m'modzi, Robinson Risner, anafotokoza momwe anakhalira masiku atatu opanda caku-dya ndi madzi. Iye adamangidwa mmunyolo mwa kuti sakadacoka. Ndipo cinthu cokweza mau cidaikidwa kunja m'khonde. Iye adapemphera kuti Mulungu apangitse kuti wailesiyo ileke kugwira nchito. Mwamsanga wailesiyo idathyoka. Mulungu adayankha mapemphero ace. Iye atangomasulidwa kucokera m'maunyalowo, patapita masiku ena, adajombulitsa nyimbo mu cilankhulo ca Morse yakuti, "ndinu wa mkuru." Mkaidi wina adaimva. Pamene iye adangotsiriza, mkaidi wina

adaikopa, "ndi kuiimbanso." Nyimbo imeneyi inali yotsimikizira cikhulupiriro ca Risner ca mwa Mulungu. Umboni wace udathandiza munthu wina kuti akhale ndi cikhulupiriro mwa Mulungu.

Lero tikhala tiri kuganizira za anthu a Cihebri ndi momwe iwo adafunira thandizo la Mulungu. Silinali loyenera kutha mwa msanga, kapena kuti cidayenera kukhala ca pafupi. Koma Mulungu adalonjeza kuwathandiza iwo ndipo Iye adasunga malonjezo ace.

(Werengani Eksodo 5:1-8,22 kukalasi)

MU BWALO LA MILANDU MWA FARAO

Pamene Mose adangodzipereka ku cifuniro ca Mulungu, iye pamodzi ndi mbale wace, Aroni, adabwerera ku Aigupto.

Iwo adaitana msonkhano wa akuru a Cihebri. Mose adawauza kuti Mulungu adakonza zofuna kuombola anthu ace. Akuruwo adakhulupirira Mose.

Kaciwiri Mose ndi Aroni adapita kwa Farao. Mulungu adawalimbikitsa kuti akaonane ndi Farao. Mose adamuza zomwe Mulungu adanena. Mulungu adafuna kupita ndi anthu ace pa ulendo wa kucipululu. Iwo adakonza phwando la cipe-mbedzo lopembedza Mulungu.

Farao adaseka anthu awiriwo ndikufunsa kuti, "Kodi Ambuye ndi ndani? Kodi ndi cifukwa ciani Ahebri ali kumupembedza? Kodi milungu ya Aigupto singacite zinthu zonse?"

Farao sanali kudziwa Mulungu wa Mose ndi Aroni. Iye anaganiza kuti ndi copusa kupe-mbedza Mulungu wosadziwika. Iye adauza Mose ndi Aroni kuti, "Ine sindimudziwa Ambuye, ndiponso sindidzalora kuti Israyeli amuke."

Kodi Mose adasiya? Werengani Eksodo 5:3-5 mu Buku Lopatulika lanu. Mose adapitiriza kupempha Farao kuti alole anthu kupita. Iye adafuna kuti Ahebri akapembedze Mulungu mu cipululu.

KUSENZETSEDWA ZOLEMERA

Farao adanena kuti Mose anali kuletsa Ahebri kugwira nchito. Iye adauza oyang'anira kuti agwiritse nchito yolimba Ahebri. "Musa-wapatsanso anthu udzu wakupanga nao njerwa monga kale." Njerwa za mu Aigupto zinali zazikuru kuposa njerwa zathu. Tsopano Ahebri anali kuyenera kudziphezera udzu wao ndi kupanga njerwa za kacurukidwe komweko. Njerwa zinali kupangidwa kucokera ku matope a mu mtsinje wa Nile. Udzu omwetedwa uja unali kuthandiza kuti zisang'ambike.

Dongosolo la Farao lidagwira nchito. Anthu a Cihebri anali ndi zilonda zambiri. Oyang'anira anali kuwakwapula cifukwa iwo sanakhoze kupanga njerwa zambiri. Atsogoleri a Cihebri adauza Farao za mabvuto ao. Farao adawapanga kuti apitenso kunchito.

Atsogoleri a Cihebri adaukira Mose ndi Aroni! Iwo adaganizira kuti Mulungu sangathe kuwapulumutsa, koma kuti zipsera zao zaonjezekera. Pamenepo Mulungu adalankhula ndi Mose. Iye adati, "Tsopano udzaona comwe ndi dzacitira Farao; cifukwa ndi dzanja langa la mphamvu adzalora kuti amuke."

MIRIRI KHUMI - KAPENA CIONONGEKO

Mulungu adatumiza miriri khumi kwa Aigupto. Mose adaneneratu za muriri uli wonse Mulungu asadatumize. Uli wonse unali